


MAFUNSO NDI MAYANKHO

AHEBRI GAWO III

 ...kukhala pano usikuuno kenanso ku kachisi, kuyembekezera mu chiyanjano chodabwitsa ichi ndi kupembedza mozungulira Mawu a Mulungu amene aperekedwa kwa ife mwaulere. Ndipo ife tiri...tikukonda kukhala otenga nawo a mdalitso uwu.

⁵⁵⁴ Ndipo ine ndikungodalira kuti Mulungu atidalitsa ife usikuuno monga Iye anachitira mmawawu, ndi uthenga wa mmawa. Ndipo ine ndimangoyankhula ndi woyandikana naye wanga, Akazi a Wood, kanthawi kapitako, ndipo ife timakambirana zimenezo, ndi Bambo Wood ndi iwo. Ndipo ine ndikukhulupirira uwo unali ulaliki wapamwamba wa M'bale Neville mwa abwino onse amene iye walalikirapo, umenewo unali umodzi umene unali wabwino kwa ine kuposa wina uliwonse umene iye anayamba walalikirapo. Ine ndithudi ndinasirira ndi kuyamikira ulaliki wodabwitsa umenewo. Ndipo iwo unandipatsa ine chilimbikitso, ndipo iwo unanditsazulira ine. Chotero ine—ine ndimakonda kuvomereza choonadi, inu mukudziwa. Chotero, za magawo olimba mtima, inu mukudziwa, kukhala wolimba mtima, ndi momwe kwa... Davide anali kumeneko, ndi momwe iye analiri... Pamene anali mu yesero lalikulu limenelo, mmalo monena kuti “Chabwino, ine ndipita ndikachite ichi, Ambuye, Inu mungondithandiza ine,” iye anayembekezera, anapita ndipo anakawafunsa Ambuye choti achite. Iye anatsitsa chapachifuwa, inu mukudziwa, ndipo anati, “Tsopano tiyeni tiyimirire ndipo timufunse Mulungu, ‘Kodi tichite chiyani mu vuto ili?’” Oh, izo zinali zolemera kwenikweni. Izo zinali ndi zonona zochuluka kuposa masitolo onse ogulitsa mankhwala omwe anali mdzikolo. Inde, bwana, izo kwenikweni zimakuchitira iwe ubwino.

⁵⁵⁵ Tsopano, usikuuno, ife—ife sitikulinga kukhala motalika kuposa pakati pa usiku, ngati ife tingathe, pa mafunso awa. Chotero ife ti—ifite tingofikira kulowa mwa iwo, pomwe pano. Ndi kumalizitsa mafunso awa, ndipo nthawi iliyonse ndikayamba kuwamaliza iwo...Tsopano, Mlongo Hattie, ine sindimatanthauza zimenezo, inu mukudziwa zimenezo. Ine—ine ndimangonena izo, mwaona; ndipo, chabwino. Koma ndiri nawo ena olimba kwenikweni pano ochokera kwa mtumiki, ndipo iwo ndi ovuta kwenikweni kuwayankha. Inu mukudziwa, alaliki amenewo, iwo amawapinda iwo mozungulira kudutsa mu Baibulo ndi kuyesera kupeza yankho lawo lawo iwo asanakufunse iwe, inu mwaona. Ndiyeno...

ndipo izi zikujambulidwa pa tepi, zikupita uko ku Georgia kwa mtumiki mzanga amene ali ndi mafunso eyiti opambana a Baibulo apa amene ali akuya kwambiri.

⁵⁵⁶ Ndipo tsopano, sabata ikubwerayi, musayiwale ndipo mutipempherere ife.

⁵⁵⁷ Ndipo mkazi wanga ali bwino; iye wadzuka tsopano, ndipo anathandizira kuphika, lero. Abwenzi athu okonedwa ochokera ku Canada, M'bale, Mlango Sothmann, ali kuno kudzatichezera, ndipo ife ndithudi tikuyamikira kutichezera kwawo. Ndipo mkazi wanga, podziwa kuti iwo akubwera, bwanji, iye anali woti adzuke kuti akhale ndi zina za zosangalatsa ndi chiyanjano cha anthu okonedwa Achikristu awa. Ndife okondwa kukhala ndi M'bale Freddie ndi ife usikuuno, ndipo iye watsala ndi. . .Iye anali pano mmawa uno, koma ine ndikukhulupirira iye watsala ndi. . .ayi, ndi choncho, iye ali ndi Meda, kuti akhale ngati ali ndi iye pamene ife tabwera kuno; chifukwa ine ndikudziwa kuti zikhala mochedwerapo pang'ono usikuuno, tikhala ndi mgonero ndi kutsukana mapazi. Chotero ndife okondwa kukhala nawo iwo ndi alendo omwe ali nafe.

⁵⁵⁸ Tsopano, tisanayambe kuyesera kuyankha mafunso. . . Ndipo mungokumbukira kuti ine—ine ndikhoza kulakwitsa, inu mwaona, ine—ine sindimadzinenera kuti ndine wolondola pa chirichonse chimene ndimachita. Ine—ine ndimayesetsa kukhala wolondola, koma mwinamwake ine ndi—ine ndikulakwitsa. Ndipo—ndipo ngati ndikulakwitsa, ndiye inu mungondikhululukira ine; ndipo ine ndikupemphera kuti Mulungu atero, nayenso, chifukwa ine sindikutanthauza kuti ndilakwitse. Ine sindimayesera kuwayankha iwo basi ku-. . .kapena momwe ine ndimango. . .mwa kukondera, ine ndimawayankha iwo mwakukhoza kwa kudziwa kwanga, mwaona. Ndipo ngati ndingasinthe malingaliro anga pa funso la Baibulo, ine ndikuganiza ndicho chinthu choyenera kuchita. Ife tikuyenera tizisinha, nthawi iliyonse, pamene Mawu a Mulungu ayankhula, chifukwa ndi Mawu a Mulungu.

⁵⁵⁹ Ndipo tsopano, ine ndikuganiza tiwapemphereranso odwala usikuuno, monga mwachizolowezi. Ndipo nthawizina iwe umangodabwa; iwe umatenga ngati kagulu kakang'ono monga aka, kocheperapo, oh, kachisi wamng'ono apa, ndipo nthawizina iwe sumawona zotsatira zomwe ungafune kuti uziwone. Koma chinthucho, chimene iwe ukuchita, iwe ukungotenga kuchokera kwa anthu thuu handirede. Ndipo umodzi wa misonkhano yaikulu, mwinamwake iwe ukukokera kulikonse kuchokera pa firii mpaka teni sauzande, inu mwaona, ndi—ndi mochulukirapo. Chotero ndiyo njira yake, iwe umayamba kuwona zambiri. Koma usikuuno, ndakhala ndikungoyankha. . .Chifukwa foni yathu imangolira mphindi zochepa zirizonse masana ndi gawo la usiku.

⁵⁶⁰ Kodi awa ndi Akazi a Reiser akhala apa, ine ndikuwayang'ana? Baibulo lanu, mlongo, Mlongo Wood ali nalo kumbuyo uko. Ine ndinalibweretsa ilo mmawa uno, ndipo ine—ine sindinakwanitse kukupatsani inu. Ndipo ine—ine sindinakuwonezi inu mmawa uno, ndipo Akazi a Wood ali nalo ilo.

⁵⁶¹ Koteru kuyankha foni ndi kupeza—a zinthu zazikulu zimene zachitika. Dona anandiyimbira ine, iye anati, “M'bale Branham, ine ndinali ku msonkhano *wakuti-wakuti* ndipo ndinakhala ndikuvutika ndi vuto *lakuti-lakuti* kwa nthawi yotalika *chomwecho*. Ndipo, inu mukudziwa, inu munangoyankhula kumbuyo uko, ndipo basi. . .” Anati, “Ine ndinatsala pang'ono kukomoka pamene Iwo unangobweretsa moyo wa kuseri.” Ndipo anati, “Ndipo ine sindinavutikenso kuyambira pamenepo.”

⁵⁶² Ndipo dona anadzabwera ndipo anati. . . Ndikukhulupirira kuti ali pano usikuuno, kapena iye amati ayendetse kuchokera ku Bedford, ine ndikukhulupirira, kapena kwinakwake kumtunda uko. Mwana wawo anali muno, ine ndikukhulupirira, amene anali ndi vuto la mtima, akuwoneka moyipa chomwecho. Ndipo iye anali atakhala muno mu msonkhano, ndipo—ndipo Ambuye anayenda mozungulira ndipo anakhudza. . . ananena kwa mnyamatayo za vuto lake, ndipo iye sankatha kukweza nkono wake, ndi vuto la mtima, ndipo nkono wake wonse unawuma, ndi mtima wake monga chonchi. Ndipo nthawi yomweyo iye analowa mu galimoto ndipo anayendetsa kupita kwawo, sanavutikepo nazo konse kuyambira pamenepo. Kodi dona uja wabwera kuno kuchokera ku Bedford? Kodi inu muli pano, dona? Ndi uyo pamenepo, kumbuyoko. Inde, iye anandiyimbira ine, kanthawi kapitako.

⁵⁶³ Ndiye pali dona anandiyimbira ine kuchokera uko mu Evansville. Ndipo sanakwanitse kufika kuno chifukwa iye ali kutali kwambiri, samadziwa kuti tikhala ndi msonkhano usikuuno wa machiritso. Ndipo anati, “M'bale Branham, ine ndinakhala mu msonkhano waku Evansville,” ndipo anati, “inu munayang'ana mmbuyo mgululo ndipo munati. . . munandiuza ine chimene ine ndinali, ndi chimene ndinali nditachichita, ndi chimene ndimavutika nacho, ndi zina zotero monga choncho.” Ndipo iye anati, “Ine ndinali ndi vuto la mphumu limenelo, ndipo ndimachita kuyatsa Chopumira cha mphumu ndi chirichonse mchipindamo kuyambira ndiri mtsikana wamng'ono.” Anati, “Izo zakhala ziri zaka ziwiri zapitazo, ndipo ine sindinakhalepo ndi dontho limodzi kuyambira pamenepo.” Mukuona?

⁵⁶⁴ Ndipo basi za iwo okha amene ali pano usikuuno, amene sanali pano mmawa uno kuti asangalale ndi umboniwo; ine ndinali ku sitolo ya ten-cent, ndimagula chidole, dzulo. Tsopano, icho sichinali cha ineyo, mwaona. Icho chinali cha mtsikana wanga wamng'ono, Rebekah, kumeneko. Ndipo—

ndipo Sarah amapitira chinachake, chimzake, lero. Ena a azimzake aang'ono akusukulu anali ndi mtundu wina wa kusonkhana pamodzi kwakung'ono, kwa tsiku lobadwa kapena chinachake, ndipo amatenga kamphatso kakang'ono; ndipo ine ndimagula chidole chaching'ono, chotalika pafupifupi *chonchi*. Ndipo apo panali dona anayenda kubwera pamenepo, anati, “Inu mukundikumbukira ine?”

565 Ndipo ine ndinati, “Sindikukhulupirira kuti ndikutero.”

566 Ndipo zinafika podziwika kuti, anali wachibale wa M'bale Neville pano, yemwe pafupifupi. . . pamene ine ndinali pa njira yanga yopita ku Sweden, iwo. . . Iye anabwera muno, anali ndi mnyamata wamng'ono mu chikuku, basi monga Edith wamng'ono apo, ndipo mnyamata wamng'onoyo anali ndi khansa, chophuka pa ubongo. Ndipo mutu wake wawung'ono unakokedwera pansu, ndipo iye. . . ndipo madokotala anali atamupatsa iye masabata atatu okha okhala moyo. Iwo anali achitulutsa icho ndipo anachiyeza icho, ndipo anawona icho chinali. . . chimene icho chinali, ndipo anangomupatsa iye masabata atatu okhala moyo. Ndipo amachita kumuyendetsa iye mozungulira mu mpando, ndipo kenako nkumuika iye pa machira pamene amapita ku chipinda ndi kukamupima iye, ndipo kenako nkudzamubweretsa iye uko. Ndinapita ndi kukamupempherera mnyamata wamng'onoyo, ndipo ndinawapempha Ambuye kuti amuchize iye. Ndipo tsiku lotsatiralo, pamene anamutengera iye kumeneko, anati, “Ine sindikufuna chikuku chimenecho.”

567 Analowa mgalimoto ndipo anakwera kumapita kumeneko, ndipo dokotala anafunzulula machira, anati, “Sindikufuna machira amenewo.”

568 Anathamangira kumeneko ndipo anakakhala pansu, adokotala anamupima iye, anati, “Chabwino,” anati, “m'malo mwa masabata atatu, ine ndikupatsa iwe zaka handiredede ndi eyiti zimene iwe uti ukhale ndi moyo.”

569 Ndipo, dzulo, amayiwo anakumana nane. Ndipo akhoza kukhala kuti ali pano, mwa zonse zomwe ine ndikuzidziwa, usikuuno. Ndipo mnyamata wamng'onoyo anali kumeneko akusewera mpira, mnyamata wamng'ono tsopano. Chotupa, khansa mu ubongo, ndipo izo zikungowonetsera. . .

570 Oh, masauzande a zinthu, mwaona. Mulungu sangalephere. Iye—Iye sangalephere basi.

571 M'bale John, kodi diso lanu liri bwino, m'bale? Iye anachita ngozi, ndipo ankakhoma msomali ndipo unamumenya iye mu diso. Ndipo ife tonse tinkawapempherera M'bale John O'Bannon, m'bale wathu wochokera ku Louisville amene anachita ngozi ndi msomali umene unamumenya iye mu diso.

572 Tsopano, mafunso awa ndi a—kuya kwa mtima wa winawake; kuti iwo anawerenga kudutsa mu Lemba ndipo

anapeza zinthu izi, ndipo iwo sama. . . mwinamwake akulephera kudzikhutitsa okha, chotero iwo adzawapereka iwo kuno kuti ife tiyesere kuwayankha. Ndipo inu mukuwona chochitika chovuta chimene izo zikutiyikamo ife; chifukwa, zimene iwe unganene, iwo angatsamire kwa izo. Chotero iwe umayenera kukhala wotsimikiza kuti ukulondola, ndipo ndine. . . motsimikiza basi momwe iwe ungakhalire. Chotero ndiye, chinthu chakuti titsimikize kuti tikulondola, tiyeni tingopempha Mzimu Woyera tsopano kuti utanthauzire izi kwa ife, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

⁵⁷³ Tsopano, Atate Akumwamba, oh, ndi mwayi wotani kunena “Atate” kwa Mlengi wamkulu wa miyamba ndi dziko lapansi. Ndipo ife tikungopempha kuti Inu mutenge mafunso awa mu chisamaliro Chanu Chomwe tsopano. Iwo anaperekedwa kuno ndi kuwonamtima kozama. Mulungu, mulole izo zibwere kuchokera mmitima yathu, kuya kwa kuwonamtima, kuti tiwayankhe iwo mopambana momwe ife tikudziwira kutero; perekani izi.

⁵⁷⁴ Ndipo mulole chifundo Chanu chikhale pa aliyense. Ndipo mulole chinachake chinenedwe pano usikuuno chimene chiti chimuthandize aliyense amene ali pano. Ndipo pamene ife tizichoka, likatha pemphero la odwala ndi kutenga mgonero ndi zina zotero, mulole tidzanene monga iwo anachokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu pamene Iye amalankhula nafe panjira?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

⁵⁷⁵ Tsopano, monga ndimanenera nthawi zambiri, kuti izi—izi apa ndi—kupambana kwa malingaliro anga pa iwo, ndiyeno nthawizina izo zimabweretsa zokambirana pang’ono. Loyamba apa, ine ndikuwona kuti ndi chinachake chimene ine ndinanenapo kale, kuti ilo laperekedwanso kachiwiri. Ine sindi. . . ndikufuna kuti ndiwerenge ilo tsopano, ngati inu mungathe.

65. Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni, kodi panali anthu ena padziko lapansi pa nthawi iyi? Mu Genesis mutu wa 5 ndi ndime ya 16, Kaini ankakhala mu dziko la Nodi ndipo anamudziwa mkazi wake.

⁵⁷⁶ Tsopano, limenelo ndi—funso lopambana. Tsopano, timaphunzitsidwa mu Baibulo. . . Ndipo nthawi zambiri izi. . . nthawizina ife mosasamala. . . Ndinkakonda kuyika kachidutswa kapepala kakang’ono, ndikuti, “Funsani. Yankhani funso lirilonse la m’Baibulo.”

⁵⁷⁷ Ndipo winawake anati, “Chabwino, kodi mkazi wa Kaini anali ndani?”

⁵⁷⁸ Oh, ndinkachita nthabwala pang’ono ndi izo kapena chinachake, ndinkati, “Oh, ameneyo anali mwana wamkazi wa apongozi ake,” kapena chinachake chonga chimenecho, inu

mukudziwa, kapena—kapena “Iye anali Akazi a Kaini.” Koma izo sizikuyankha funsolo. Apo pali . . .

579 Kumeneko Kaini anali ndi mkazi, chifukwa Baibulo limati anali naye. Ndipo ngati Kaini anali ndi mkazi, iye ankayenera kuti akamutenge iye kwinkwake. Ndipo izi zingalumikizane bwino mu izi apa:

Kodi panali anthu ena padziko lapansi pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mmunda wa Edeni?

580 Tsopano, ngati inu mungazindikire, mu Baibulo si kawirikawiri pamene zinkalembedwa za mkazi akamabadwa. Nthawizonse ndi mwana wamwamuna amene amalembedwa mu Baibulo, osati mkazi. Kawirikawiri sizimatchulidwa konse za kubadwa kwa mwana wamkazi, mu Baibulo. Kapena, moona, sindikudziwa ngati ndingakumbukire mmodzi pompano, mmalingaliro, pamene analembapo kubadwa kwa mwana; anati, “Iwo anabala ana aamuna ndi aakazi.”

581 Tsopano, Baibulo limangokamba za ana atatu amene anabadwa kwa Adamu ndi Eva, ndipo ameneyo anali Kaini, Abele, ndi Seti. Tsopano, ngati atatu onsewo anali amuna, ngati kunalibe akazi aliwonse amene anabadwa, ndipo pamene mkazi yekhayo (Eva) anafa, mtundu wa anthu ukanasiya kukhalapo nthawi yomweyo, chifukwa sipakanakhala njira kwa iwo kuti—kuti akhale ndi chirichonse . . . mtundu wa anthu kuti uzipitirira, chifukwa pakanakhala popanda akazi otsalira. Eva akanakhala yekhayo. Koma, inu mwaona, iwo samalemba a—kubadwa kwa ana aakazi, mu Baibulo, chotero chomwecho iwo ankayenera kukhala ndi atsikana mofanana ndi anyamata.

582 Tsopano, wolemba wakale, mmodzi wa olemba akale kwambiri omwe ife tiri nawo, Josephus, amanena kuti iwo anali ndi ana sevente, ndipo Adamu ndi Eva; m’modzi wa olemba akale kwambiri, “ana sevente, ndipo iwo onse anali ana aamuna ndi aakazi.”

583 Tsopano, ngati . . . Ndiyeno ngati Kaini anapita ku dziko la Nodi . . . Tsopano, ngati inu mungazindikire, wolembayo anali kwambiri, amalemba mwaluntha kwambiri apa. Kodi inu munazindikira momwe iye anabwerezera izo?

Mu Edeni, pamene iwo anali ndi ana awo mu Edeni . . .

Tsopano, osati m’unda wa Edeni, wolembayo amadziwa zimenezo. Aliyense amene analemba cholemba apa, anati:

Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni . . .

584 Osati mmunda wa Edeni, chifukwa iwo anali atathamangitsidwa mmunda wa Edeni. Koma iwo anali adakali mu Edeni, ndipo munda wa Edeni unali kum’awa kwa Edeni. Koma Edeni anali ngati dera kapena—kapena chiyani . . . kapena dziko, ndipo kenako Nodi linali dziko lina kapena dera pafupi ndi ilo.

585 Tsopano, munthu yekhayo amene Kaini akanakhala naye, kapena akanamukwatira, akanayenera kukhala mlongo wake yemwe. Iye ankayenera kutero. Chifukwa pali mwamuna ndi mkazi mmodzi yekha amene iwo akanachokerako, mwaona, ndipo iye ankayenera kuti akwatire mlongo wake yemwe. Tsopano, izo zinali zovomerezeka mmasiku amenewo.

586 Ndipo Isaki anakwatira msuweni wake woyamba wa magazi, Rebekah, wodzozedwa ndi Mulungu. Sarah anali mlongo wake wa Abrahamu, mlongo wake wamagazi; osati mwa amayi ake, mwa abambo ake. Mwaona, mlongo wamagazi amene—amene Abrahamu anamukwatira; mayi wosiyana, koma bambo yemweyo.

587 Chotero, inu mwaona, kukwatirana pachibale nthawi imeneyo, zisanachitike—mtsizje wa magazi usanafowoketsedwe mu mtundu wa anthu, zinali zovomerezeka ndi zabwino. Tsopano izo sizololezedwa. Ngati ungakwatire mlongo wako lero, ndi kukhala ndi ana, iwo mwinamwake angakhale... chabwino, iwo angakhale olumala ndi chirichonse. Ngakhale kutsika kwa msuweni woyamba ndi wachiwiri sakuyenera kukwatirana, mwaona, chifukwa mpita wa magazi ukumakhala wotsika ndipo ukumayenda mofooka.

588 Koma chinthu chokhacho ndiye chimene Kaini akanachita, chikanakhala, kukwatira mlongo wake yemwe. Ndipo pamenepo ndi pamene ana anali kuti...Iye anamutenga mkazi wake, anapita ku dziko la Nodi ndipo anamudziwa iye, ndipo kuchokera pamenepo panadzabwera a—ana. Mwaona, a... .

589 Ndipo ngati inu mungazindikire, kuchokera mu mzere wa Kaini kunadzabwera amuna anzeru. Kuchokera mu mzere wa Seti munadzabwera amuna achipembedzo, ine ndikutanthauza, a—mpesa wa chilungamo. Pomwepo, awiri amenewo, anabweretsa mzere womwewo umene ife tikukhalamo lero.

590 Ngati mungazindikire lero (pongomalizitsa funso ili): mzere uja wa Kaini ukadalipobe, ndipo mzere wa Seti ukadalipobe. Iwo onse awiri anabwera motsika mofanana basi. Ana a Kaini ali muno mu Jeffersonville usikuuno, ndipo ana a Seti ali muno mu Jeffersonville usikuuno. Pamene mpita wa magazi ukufooka ndi kumatuluka, koma mzere umenewo udakalipobe.

591 Tsopano, penyani. Ana a Kaini nthawizonse anali... ndipo chiwonongeko cha chigumula chisanachitike, iwo anali anthu anzeru: asayansi, ophunzitsa; ndi achipembedzo kwambiri, koma linali gulu lotsutsidwa. Mukuona? Tsopano penyani, iwo anali ngati atate wawo Kaini. Kaini, iye anali munthu wachipembedzo. Iye anamanga guwa lokongola, ndipo anapanga mpingo wokongola, ndipo anayesetsa kuti azipange izo ziziwoneka zokongola kuposa ntchito yaying'ono ija imene Seti anali nayo kumusi uko. Kodi inu mumadziwa

zimenezo? Iye ndithudi... Anakongoletsa guwa ndi maluwa, ndipo analikongoletsa ilo, ndipo analipanga ilo liziwoneka lokongola; ndipo anapanga tchalitchi chopambana, chachikulu, chodzadza, chifukwa iye ankaganiza kuti akanakonderedwa ndi Mulungu pochita zimenezo.

⁵⁹² Ndipo Abele anapita ndipo anakatenga mwana wa nkhusa, ndipo anayamba kumukokera iye ku guwa, ndipo anakamuyika iye pa thanthwe ndi kumupha iye.

⁵⁹³ Ndipo tsopano, ngati Mulungu ali wolungama, ngati zonse zomwe Iye ankafuna zinali kupembedza, Kaini anamupembedza Mulungu moona mtima monga mmene Abele ankachitira. Awiri onsewo anali owonamtima. Awiri onsewo anali kuyesetsa kuti apeze chisomo ndi Mulungu. Iwo sanali mmodzi wa iwo osakhulupirira. Awiri onsewo anali, mwamtheradi, okhulupirira mwa Yehova. Tsopano, pamenepo, zimenezo zikutipatsa ife chinachake choti tichiganizire.

⁵⁹⁴ Ena pano usikuuno ine sindinawawonepo, anthu; ine sindinakuwonenipo inu. Koma inu mukuyenera kuzindikira ichi, ndipo muchisunge ichi mmalingaliro anu. Mukuona? Ziribe kanthu momwe iwe uliri wachipembedzo, izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi zimenezo. Iwe ukhoza kumakhala mu tchalitchi, ukhoza kumakhala woonamtima nthawizonse, ndipo iwe wataikabe! Mukuona?

⁵⁹⁵ Ndipo inu mukuti, “Chabwino,” inu mukuti, “abusa athu ndi anzeru kwambiri, iwo anabwera kudzera m’maseminare kuti akalandire maphunziro abwino kwambiri. Iwo ndi azaumulungu, iwo amadziwa zonse—zaumulungu zonse ndi zina zotero. Ndipo iwo ndi anzeru, ophunzitsidwa, kwambiri... osankhidwa bwino kwambiri amene ife timawadziwa.” Ndipo iwo akhoza kutayikabe! Mukuona?

⁵⁹⁶ Tsopano Kaini, pa mzere wake: iwo anali, mmodzi aliyense, achipembedzo kwambiri; anthu otchuka kwambiri; ndipo iwo anali asayansi, ndi madokotala, ndi omanga, ndi ogwira ntchito, ndi amuna anzeru. Koma mzere wonsewo unakanidwa, kuchokera kwa Kaini mpaka mmusi.

⁵⁹⁷ Ndipo ku mbali ya Abele: iwo sanali omanga kapena ophunzitsa kapena munthu wanzeru; iwo anali, mochuluka kapena motsika, odzichepetsa, ngati oweta nkhusa, ndi osauka, amene ankangoyenda mwa Mzimu.

⁵⁹⁸ Tsopano, Baibulo limati, “Palibe kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene samayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu.” Munthu wauzimu amakhala ndi mzimu wauzimu umene sungafe. Ndipo munthu wachithupi amakhala ndi chikhalidwe chachipembedzo pomuzungulira iye (ndipo amafuna kuti azipembedza ndi zina zotero) koma ndi wachithupi; osati wosakhulupirira, koma wokhulupirira wachithupi; ndipo unali mtundu umene unakanidwa.

⁵⁹⁹ Tsopano, kuchokera pamenepo, Kaini anapita ndipo anakawatira mkazi wake mu dziko la Nodi. Tsopano, ilo silimanena amene Seti anakwatira, kapena amene ena anakwatira. Ndipo chinthu chokongola kwambiri cha izo ndi kudziwa kuti—kuti, Kaini kukwatira, tiri nalo yankho kwa izo. Chifukwa iye ankayenera kumukwatira mlongo wake, kapena iye . . . kapena pakanakhala a . . .

⁶⁰⁰ Panalibenso akazi pa dziko lapansi, koma basi ankangoyenera kuti achokere kwa Eva. Iye anali mayi wa amoyo onse. Ndizo, anthu onse amene anali moyo, iye anali mayi wa iwo. Ndi chifukwa chake iye anali . . . Mawu akuti *Eva* amatanthauza “mayi wa amoyo.” Chotero iye anabwera ndipo anabala mwana uyu. Ndipo Kaini anakwatira mlongo wake yemwe, ikanakhala njira yokhayo imene ine ndikanati ndiwonere izo. Chotero panali anthu amene ankakhala mu tsiku limenelo, moonadi. Mukuona? Chabwino, ndi . . .

Pamene Adamu ndi Eva anali ndi ana awo mu Edeni . . .
Tsopano penyani, ndiro funsolo: **Pamene iwo anali ndi ana awo mu Edeni, kodi panali anthu ena padziko lapansi panthawi iyi? Ayi! Ndiye mu Genesis 5:16, inu mwaona, Kaini anakakhala mu dziko la Nodi ndipo anamudziwa mkazi wake.** Ndithudi. Mukuona?

⁶⁰¹ Ameneyo ndi Genesis 1, pamene Iye anamulenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe, chimene chinali mu fiofane. Ndipo mu Genesis 2, Iye anamupanga munthu kuchokera ku fumbi la dziko lapansi, yemwe anali munthu waumunthu amene ife tiri naye tsopano. Ndipo kenako, mu 3 munali kugwa, ndipo anathamangitsidwa kuchokera mmunda wa Edeni; ndipo ana anabala ana. Ndipo Kaini anamutenga mkazi wake ndipo anakakhala naye mdziko la Nodi, kunja, chifukwa Mulungu anali atamulekanitsa iye ku chiyanjano ndi m’bale wake yemwe (chifukwa cha imfa ya—ya Abele). Ndipo uyo ndi amene iye anali naye, mlongo wake yemwe, ndipo anamukwatira iye; ndi njira yokhayo imene ine ndingathe, inemwini, ndingathe kuwona momwe kuti—iye anakwatirira.

⁶⁰² Tsopano, izo zinanenedwapo . . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti azimzanga achikuda amene ali muno andikhululukira chonena ichi, chifukwa mwamtheradi icho si choona. Nthawi yoyamba imene ine ndinayamba ndakumanapo ndi aliyense mmoyo wanga, nditatembenuka mtima . . . Ine ndinali . . . ndinakomana ndi M’bale George DeArk ndi iwo kumeneko. Ndipo ndinayenda, ndipo Ambuye ananditsogolera ine ku malo aang’ono. Ndipo iwo anakambirana kumene munthu wachikudayo anachokera. Ndipo iwo ankayesera kunena kuti munthu wachikudayo, kuti Kaini anakwatira chinyama chonga nyani, ndipo kupyolera pamenepo panadzatulukira mtundu wachikuda. Tsopano, izo nzolakwika! Mwamtheradi, izo nzolakwika! Ndipo musadzaziyimire konse zimenezelo. Chifukwa

kunalibe wachikuda kapena woyera, kapena wina aliyense wosiyana, ndi mtundu umodzi wokha wa anthu mpaka ku chigumula. Ndiye chitachitika chigumula ndi nsanja ya Babulo, pamene iwo anayamba kumwazikana, ndi pamene pamene iwo anatenga mitundu yawo ndi zina zotero. Iwo onse anabwera kuchokera ku mtengo womwewo. Ndiko kulondola ndendende. Adamu ndi Eva anali abambo ndi amayi, padziko lapansi, a cholengedwa chirichonse cha anthu amene anakhalapo padziko lapansi. Uko nkulondola. Wakuda, woyera, wotumbululuka, wofiirira, wachikasu, mtundu uliwonse umene inu mungakhale, amenewo mwamtheradi ndi malo kumene mumakhalako, ndi momwe izo—izo. . . Monga ngati. . .

⁶⁰³ Ine ndikuganiza kuti ndikhoza kufotokoza izi pamene ndiri pa izo. Anthu apa tsopano mu tsankho ili ndi malamulo ndi zinthu zomwe iwo akuzivomereza, ine ndikuganiza ndi zopusa. Ine ndikutero kwenikweni. Mvetserani, ingowasiyani anthu amenewo okha, iwo akudziwa zimene iwo akufuna. Mulungu anamupanga munthu wachikuda, ndipo iye amasangalala nazo izo. Mwamtheradi! Ngati Mulungu akanandipanga ine kukhala munthu wachikuda, ine ndikanakhala wokondwa nazo izo; ngati Iye akanandipanga ine munthu wabulauni, ine ndikanakhala wokondwa; ngati Iye anandipanga ine mzungu, ndine wokondwa; ngati Iye akanandipanga ine munthu wachikasu, ine ndikanakhala wokondwa. Mulungu anatipanga ife mu mitundu yathu, ndipo Iye anatipanga ife momwe Iye ankatifunira ife, ndipo ife tonse ndife ana Ake. Mwamtheradi! Ndipo iwo sayenera kuti azikangana ndi kumapitirira monga choncho. Uko nkulakwa kuchita zimenezo. Iwo sakuyenera kumachita zimenezo. Mulungu anatipanga ife. . . momwe timazifunira izo.

⁶⁰⁴ Ndipo munthu wachikuda, iye samafuna kuti apite kunja uko ndi kukaswa wake—kam’badwo kake kapena mtundu wake, ndi kuzisakaniza izo mu zoyera ndi chirichonse monga choncho. Ine sindikumuyimba mlandu iye. Ine sindikutero. Munthu wachikuda ali ndi zinthu zomwe mzungu alibe nkomwe. Mwamtheradi! Ndiko kulondola ndendende. Ndipo Mulungu sanafune kuti iwo azikhala mwanjira imeneyo.

⁶⁰⁵ Chabwino, taonani. Munthu wachikuda ndi. . . iye—iye ndi. . . iye ali ndi—ali ndi malingaliro a iye omwe mzungu alibe. Ali amakhala ndi kukondwa kopereka mwayi, a “amadalira Mulungu, ndipo amangozisiya zina zonsezo kuti zizipita”; kaya iye ali nazo kapena iye alibe, iye amakhala wokondwa mulimonse. Ine ndikufuna nditakhala ndi zochuluka zonse za izo, usikuuno, ine ndithudi ndikutero. Chabwino, iye ali nazo izo, ndipo ndicho chuma chake; iwo samafuna kuzisakaniza izo ndi mtundu wina ndi kuziswa izo, chonchobe. Ndiko kulondola ndendende.

⁶⁰⁶ Ine ndikuganiza dona kumusi uko ku Shreveport anapanga

imodzi mwa zopambana—ndemanga zopambana zimene ine ndinazimvapo m'moyo wanga. Iye anapanga ndemanga, ndipo iwo anailemba iyo mu pepala. Iye ananyamuka, iye anati, “Momwe zinthu izi zikuchitikira kuno, mu tsankho ili, sindikufuna kuti ana anga azipita ku sukulu uko ku sukulu ya azunguyo.” Anati, “Iwo sangachipeze tcheru chomwe akanakhala nacho ngati iwo akanakhala ndi mphunzitsi wachikuda.” Mkazi ameneyo ndi mkazi wanzeru. Iye ankadziwa chimene ankakamba, iwo amapeza maphunziro abwinoko. Ndiko kulondola ndendende. Chotero ine ndikuganiza anthu amalakwitsa pochita zimenezo.

⁶⁰⁷ Ndiyeno iwo amati, “Kaini ndi Abele...” ndi ena otero monga choncho. Ayi, bwana! Mtunduwo unalibe kanthu kochita ndi izo. Ndi mzimu mkati mwake umene uli ndi chochita nazo. Ndiko kulondola ndendende.

⁶⁰⁸ Chotero Kaini anamudziwa mkazi wake, ndipo ameneyo anali mlongo wake. Ndipo iwo... anamutengera iye ku dziko la Nodi, ndipo kumeneko kunatulukira mitundu ikuluikulu ya dziko lapansi: achipembedzo ndi opembedza.

⁶⁰⁹ Ndipo tangoganizani lero, mzanga, mungoyima ndi kuganiza kwa mphindi yokha. Kuti pali ma teni amasauzande kuchulukitsa mateni amasauzande ndi masauzande a masauzande, a mwamtheradi anthu opita ku tchalitchi, basi owonamtima ndi odzipereka kwa mpingo umenewo momwe iwo angakhalire, izo ndi zotayika motalikira basi monga Kaini anali. Mukuona? Ndi Mulungu Amene amasankha! Ndi Mulungu Amene amasankha! Mukuona? Mulungu Amene amapereka chifundo! Dongo silinganene kwa woumba, ndi woumba pamwamba pa dongo. Uko nkulondola.

⁶¹⁰ Tsopano apa pali lokongola, lotsatira apa:

Mu Petro Wachiwiri 2:4—2:4 . . .

⁶¹¹ Winawake ali ndi Baibulo, akufuna kuti atembenezire ku Malemba awa mofulumira ndithu pamene ine ndikuwerenga Iwo, ngati inu mukufuna kutero, ndi kukhala ngati mundithandize ine motsatira apa, pamene ife tikutenga funso ili.

⁶¹² Tsopano, pa Kaini uyu ndi—ndi zina zotero, ngati izo sizikukhutitsa izo tsopano, inu mungotilola ife tikhale nazo izo. Ife tikhala okondwera . . .

⁶¹³ Tsopano Petro Wachiwiri 2:4. Chabwino, bwana, ife tiri pamene:

66. Petro Wachiwiri 2:4, “Pakuti ngati Mulungu wa . . . Pakuti ngati Mulungu sanalekerere angelo amene anachimwa, koma anawaponyera iwo ku gehena,” ndiye nchifukwa chiyani Khristu analalikira kwa mizimu yomwe ili mndende, mu Petro Woyamba 3:19?

614 Tsopano, ife tapeza Petro 2:4, poyamba. Chabwino:

Pakuti ngati Mulungu sanalekerere angelo amene anachimwa, koma anawaponyera iwo pansi—pansi ku gehena, ndioi—ndipo anawapereka iwo ku unyolo wa mdima, kuti asungidwe kufikira chiweruzo;

615 Tsopano, tsopano tiyeni tipeze mu Petro Woyamba (uyo ndi Petro Wachiwiri), Petro Woyamba 3:19, mvetserani kwa izi. Ndi ife apa, pomwe pano. Izi zangobwera kumene, chifukwa chimene ine sindinazilembe izo.

...amene aponso...anapita ndi kukalalikirira kwa mizimu imene inali m'ndende;

616 Oh, inde, ndi ife apa. Tiyeni tiyambire pang'ono izo zisanachitike, ndime ya 18:

Pakuti Khristu nayenso...anazunikapo kamodzi chifukwa cha machimo, wolungama chifukwa cha osalungama, kuti iye akatifikitse ife kwa Mulungu, wophedwa mu thupi, koma wofulumizitsidwa ndi Mzimu:

Momwenso Iye anapita ndipo anakalalikirira kwa mizimu imene inali m'ndende;

Imene nthawi yina inali yosamvera,...

617 Mzanga wokonedwa, ngati ukanangowerenga ndime yotsatira, ndipo apo Iwo anafotokoza zimenezo. Mukuona?

Imene nthawizina inali yosamvera, imene kuleza mtima kwa Mulungu kunadikirira m'masiku a Nowa, pamene chombo chinkakonzedwa, m'menemo ochepa, ndiwo, miyoyo isanu ndi itatu inapulumutsidwa ndi madzi. (Mukuona?)

618 Tsopano, ngati inu mungazindikire umu, ine ndikuganiza mlaliki uyu ali ndi lina pa...chinachake pamzere womwewo, chiyankhidwa patsogolo pang'ono.

619 Petro Woyamba 4...kapena 2:4, ngati mungazindikire, “pakuti ngati Mulungu sanalekerere angelo,” kodi *mngelo* ameneyo walembedwa bwanji? Chilemba chaching'ono “m.” Mukuona? Tsopano, cha apa, “mizimu imene inali m'ndende imene sinalape mu kuleza mtima kwa masiku a Nowa,” angelo omwewo. Anali amuna: atumiki, alaliki; “sanawalekerere angelo.” Kodi inu mumadziwa kuti a...mawu akuti *mngelo* amachokera ku mawu akuti “mtumiki”? Ndi angati amadziwa kuti *mngelo* ameneyo ndi “mtumiki”? Mwamtheradi, *mngelo* ndi mtumiki, “ndipo Iye sanawalekerere angelo.” Mukuona?

620 Ndipo cha apa mu Ahebri, inu mukukumbukira ife tinadutsa mu izo masabata angapo apitawo, “angelo”?

621 Ndipo cha mu Ahe...mu Chivumbulutso, “Kwa *mngelo* wa mpingo wa ku Sarde lemba zinthu izi. Kwa *mngelo*

wa mpingo wa ku Efeso lemba zinthu izi. Kwa mngelo wa mpingo . . .” Mukukumbukira zimenezo? Ndipo tiliyenditse liwu lakuti *mngelo* mmbuyo, ndipo kuchokera mu dikishonare, ndi kukapeza kuti ilo limatanthauza “mtumiki.” Iye akhoza kukhala “mtumiki pa dziko lapansi, mthenga wauzimu,” liwu lakuti *mngelo*.

⁶²² Chotero mu chikhalidwe ichi, ngati tingatenge lexicon ndi kuliwendetsa ilo mmbuyo, inu mudzapeza kuti zimayambira pa “amithenga, amithenga oyamba.” Onani, “Ngati a . . . Ngati Iye sanalekerere . . . Pakuti ngati Mulungu sanalekerere angelo amene anachimwa,” (Mukuona?) “ndi zolengedwa zauzimu,” (Mukuona?) “atatha kudikirira . . .”

Tsopano penyani, iye anati:

. . . ngati . . . sanalekerere angelo amene anachimwa, koma anawaponyera iwo ku gehena, ndipo anawapereka iwo ku unyolo wa mdima, kuti akasungidwe kufikira chiweruzo;

⁶²³ Ndiye tayang’anani mu Petro Woyamba apa kachiwiri, 3:19, penyani momwe izi zikuwerengekera tsopano:

Pakuti mmenemonso iye anapita ndipo anakalalikira kwa mizimu m’ndende;

Imene nthawi ina inali yosamvera, pamene kuleza mtima kwa Mulungu kunadikirira m’masiku a Nowa, . . . (mwaona, anali atumiki a tsiku limenelo, atumiki) . . . pamene chombo chinkakonzedwa, momwemo . . . ndiko kuti, miyoyo isanu ndi itatu inapulumutsidwa ndi madzi.

⁶²⁴ Tsopano ngati inu mungazindikire pamene zolengedwa izo zinali Kumwamba. Tsopano, uko mu Chivumbulutso 11 . . . kapena mutu wa 7, ine ndikukhulupirira . . . kapena ayi, ayi, ndi mutu wa 12. Iye akupereka chithunzi cha mkazi atayima; mwezi uli pamutu pake ndi dzuwa . . . kapena, dzuwa kumutu kwake, ndi mwezi pansu pa mapazi ake. Ndipo chinjoka chofiira chinayima kuti chimulikhwire Mwanayo mwamsanga pamene Iye abadwa, ndipo icho chinatenga mchira wake, ndipo chinakoka limodzi la magawo atatu a nyenyezi za Kumwamba ndi kuziponyera padziko lapansi. Kodi munazindikira zimenezo? Tsopano, izo sizikutanthauza kuti Satana ali ndi—mchira wautali umene iye amawakola nawo anthu, koma “nthano imene iye *ananena*,” ndipo anakoka gawo limodzi mwa magawo atatu a nyenyezi zimenezo. Nyenyezi zimenezo zinali mbewu ya Abrahamu.

⁶²⁵ Abrahamu anati, “Oh . . .”

⁶²⁶ Mulungu anamuza Abrahamu, “Tayang’ana mmiyamba, ndipo uwerenge nyenyezi ngati iwe ungate.”

⁶²⁷ Iye anati, “Ine sindingathe kuchita zimenezo.”

628 Iye anati, “Ndipo sudzathanso kuwerenga mbeu yako,” nyenyezi.

629 Kodi Nyenyezi Yowala ndi Yammawa ndi Ndani? Yesu waku Nazarete, wowala kwambiri yemwe anayamba wakhalapo mu thupi la munthu. Iye ndi Nyenyezi Yowala ya Mmawa. Ndipo Iye ndi Mbewu ya Abrahamu, akubwera kudzera mwa Isaki. Ndipo ife, pokhala akufa mwa Khristu, timatenga Mbewu ya Abrahamu ndipo ndife olandira monga mwa lonjezo.

630 Chotero nyenyezi zakumwamba zinkayimira mizimu ya anthu kuno. Ndipo pamene chinjoka chofiira (Roma, pansi pa kuzunzidwa kwake) chinakumbatira mu magawo awiri pa atatu a . . . kapena gawo limodzi mwa magawo atatu a nyenyezi, ndi kuziponyera izo pansi, apo panali pa kupachikidwa kwa Ambuye Yesu wathu pamene iwo anamukana Iye ndipo Iye anali . . . ndipo anamutulutsa Iye kunjira ndipo analibe kanthu kochita ndi Iye; pamenepo panali gawo lachitatu lija la nyenyezi zaungelo, zolengedwa zaungelo.

631 Mwaona, mu thupi lanu, mkati mwanu . . . (ife tiri ndi funso lina pa izo, mwachindunji, kuti tiyankhe ilo bwino). Chotero pamene . . . Mkati mwanu muli mzimu, munthu wina. Kunja kwa inu kuli munthu mmodzi, mkati mwanu muli munthu wina. Chotero mkati mwanu muli chazimu, kunjira kwanu ndi chathupi. Mukuona? Ndipo munthu uyu, ngati inu muli wotsogozedwa ndi Mzimu, ndi Mulungu, inu munadzakhala mtumiki wa Mulungu, kapena mngelo. *Mtumiki* wa Mulungu, *mngelo* wa Mulungu, ndi mawu omwe omwewo; simungawalekanitse iwo: mtumiki wa Mulungu, kapena, mngelo wa Mulungu.

632 Ndipo ndi ndani amakhala ndi ulamuliro waukulu? Mngelo wochokera Kumwamba kapena mngelo pa guwa? Ndi ndani ali nawo? Mngelo pa guwa! Paulo anati, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba adzabwera ndi kudzalalikirira kwa inu uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu umene ndaulalikirira kale, mulole iye akhale wotembereredwa.” Chotero mngelo wodzozedwa ndi Mzimu Woyera ndi Mawu amaima pafupi ndi Mulungu. Uko nkulondola. Kumwamba, ulamuliro wake . . .

633 “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zinaperekedwa mdzanja Langa. Pita, ndipo Ine ndidzapita nawe. Chirichonse chimene udzamanga padziko lapansi, Ine ndidzachimanga Kumwamba. Chimene udzamasula pa dziko lapansi, Ine ndidzachimasa Kumwamba.”

634 Oh, ngati Mpingo waukulu woyera ukanangozindikira mphamvu yake yochitira zinthu izi! Koma pali kukayikirira kwakukulu ndi mantha ndi kunjenjemera, kudabwa ngati zidzatero, “Kodi izo zingachitike?” Bola ngati izo ziripo, Mpingo sungayime mowongoka. Ndipo pamene kuyankhula kulikonse kwa mantha kuchoka ndipo Mzimu Woyera ukulamulira

kwathunthu Mpingo, ndiye mantha onse amachokapo, ndipo Mpingo umenewo umakhala ndi mphamvu. Mukuona? Bwanji, iwo amakhala ndi chirichonse chimene Kumwamba chimakhala nacho kumbuyo kwawo. Iwo ndi akazembe a Mpandowachifumu. Mwamtheradi! Kazembe wa Khristu amakhala ndi ulamuliro, ndipo chirichonse chimene Khristu ali nacho ndi cha kazembeyo. Ndipo Iye anati, “Pitani inu ku dziko lonse lapansi, inu ndi mboni Zanga Mzimu Woyera ukadzabwera pa inu.” Ndipo kodi mboni ndi chiyani? Ndi kazembe; ndi kubwera kudzachitira umboni chinachake. Mphamvu zonse za Kumwamba ziri mmanja mwanu momwe! Oh, nchifukwa chiyani ife timakhala? Ndipo mpingo ndi wosabala, ndipo ife timakhala osachita kanthu. Ndi chifukwa chakuti ife sitimazindikira zinthu izi.

⁶³⁵ Tsopano, miyoyo imene inali mu ndende (imene sinalape), sinali Angelo owoneka amene anali—atatsitsidwa pansu mu mawonekedwe a Angelo, koma inali mizimu ya zolengedwa zaungelo zomwe zinagwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe, kumbuyo uko pamene nkondo inkachitika Kumwamba. Ndipo Satana ndi—ndi chinjoka anamenyana, ndipo kenako . . . kapena Mikaeli ndi—ndi—chinjoka anamenyana (ndi Lusifara). Ndipo Lusifara anaponyedwa kunja pamodzi ndi ana ake onse (angelo onse amene iye anawanyenga), ndipo angelo amenewo anadza ku dziko lapansi ndipo analamulidwa pamenepo kuti adzakhale anthu. Ndipo pamene iwo anatero, ndi pamene “ana aamuna a Mulungu anawona ana aakazi a anthu kuti anali okongola, ndipo anadzitengera kwa iwo akazi.”

⁶³⁶ Iwo ndi ana a Mulungu. Munthu aliyense amene wobadwa mdziko lino ndi mwana wa Mulungu. Mosalabadira kuti iye ndi wochimwa kapena chimene iye ali, iye ndi mwana wa Mulungu. Wolengedwa mchifanizo cha Mulungu kwa matamando a Mulungu, iye analengedwa mwanjira imeneyo. Koma Mulungu pachiyambi ankadziwa amene akanati adzamulandire Iye ndi amene akanati asadzamulandire Iye. Chotero Iye akanakhoza kukonzeratu, kapena, osati kukonzeratu, koma mwa kudziwidwiratu Iye akanakhoza kudziwa yemwe akanati adzapulumutsidwe ndi yemwe akanati asadzapulumutsidwe, pakuti Iye ankadziwa munthu amene akanati adzatenge mzimu uti.

⁶³⁷ Ndipo mizimu imeneyo imene imachokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo imayima patsogolo pa Mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo inakhala . . . ndi mabillioni ndi mabillioni ndi manusu a nthawi dziko lisanayambe nkomwe, mu Kukhalapo kwa Mulungu, kodi mukuganiza kuti iwo samadziwa kanthu za kupembedza? Ndipo iyo inabwera pansu ndi kudzalowa mwa munthu momwe, ndipo iwo amapembedza Mulungu! Mwamtheradi, amapembedza Mulungu; ndipo iwo ali ndi chidziwitso cha Mulungu, ndipo

iwo ndi anzeru, ndi othyathyalika, ndi ophunzira, nthawizonse. Koma Mulungu anawakana iwo kuyambira pachiyambi!

⁶³⁸ Chotero choncho, mzanga, umembala wa mpingo, kapena—kapena chidziwitso cha zaumulungu zina kapena chinachake, ziribe kanthu kamodzi kochita ndi Izo. Iwo akuyenera kukhala Magazi a Yesu Khristu ndi kubadwa kwatsopano kumene kumakulumikizani inu kwa Iye ngati munthu mmodzi. Ndi zimenezotu.

⁶³⁹ Mulungu, pachiyambi pamene Iye anadziwa kuti... Amuna ndi akazi anapangidwa mmodzi, osati awiri, iwo anapangidwa mmodzi. Iwo analekanitsidwa, mmodzi anayikidwa mu thupi ndipo wina mu fiofane. Iye ankadziwa zimenezo. Chotero kuti atsimikizire izo kwa inu: pamene Mulungu anamupanga mkazi, Iye sanatenge dothi lina ndi kumupanga iye monga Iye anachitira ndi mwamuna; Iye anatenga nthiti kuchokera ku mbali ya Adamu, ndipo iye anadzakhala chotuluka kuchokera kwa mwamuna (chifukwa mkaziyo ndi gawo la mwamuna). Inu mukumvetsa Zimenezo tsopano? Mukuona? Ndi zimenezotu.

⁶⁴⁰ Ndi amenewo angelowo. Ndipo Mulungu ndi mzimu umene walumikizidwa ndi Mulungu amakhala Mzimu umodzi. Uko nkulondola. Tsopano, Mzimu wa Mulungu umene umakhala mu Mpingo, ndi Mzimu umene umachokera Kumwamba, umene Mulungu anawudziwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe, umene unakana bodza la mdierekezi. Ndipo mzimu umenewo un kayenera kutenga thupi la mnofu kuti udzakhale... udzatenge mayeso ake. Iye an kayenera kubwera mnofu monga ena awa anachitira, ndipo onse a iwo ayikidwa pa goli lofanana. Ndipo Mulungu, pachiyambi, ankadziwa mizimu imene ikanadzatero, ndi yomwe sikanadzatero. Ndi zimenezotu. Mdierekezi ameneyo ndi wanzeru kwambiri iye akanadzanyenga osankhidwa omwe, ngati kukanakhala kotheke.

⁶⁴¹ Chotero mizimu iyi, angelo awa amene analalikira, anali mu ndende; *angelo*, ngati mungazindikire izo apa, ndi chilembo chaching'ono “a” zimene zikutanthauza “munthu”; angelo, amithenga pano padziko lapansi. Iwo anachimwa, ndipo njira yokhayo imene iwo akanachimwa ndiyo kusakhulupirira! Ndipo momwe... Iwo anali ndi zipembedzo zawo, ndipo iwo sanakhulupirire uthenga wa Nowa. Iwo sanakhulupirire uthenga wa Enoki. Ndipo iwo anawukana Uthenga wawo, “ndipo anatsutsidwa,” Baibulo linati iwo anatero.

⁶⁴² Enoki ananenera kwa iwo, anati, “Ambuye akubwera ndi ma teni sauzande a oyera Ake.”

⁶⁴³ Ndipo iwo ananenera. Ndipo Nowa anamanga chombo, ndipo iwo anati, “Iye ndi woyera- wozigudubuzo! Iye ndi wotengeka! Palibepo chinthu ngati mvula ikubwera.” Ndipo zaka handirede ndi twente zinadutsa, ndipo iye anali ndi chipembedzo chimene chinali ndi chipulumutso mwa icho,

panali njira yothawirapo imene inapangidwa, koma iwo anali okhutitsidwa ndi chikhalidwe chawo.

⁶⁴⁴ Umo ndi momwe izo ziriri lero, kuti munthu akukhutitsidwa mu chikhalidwe chawo. Koma ilipo njira yothawira, ndipo njira imeneyo ndi kudzera mwa Yesu Khristu. Amen. Ndi zimenezotu apo: fuko lomwelo, mizimu yomweyo.

⁶⁴⁵ Ndipo iwo anali mwamtheradi anthu achipembedzo, achipembedzo kwambiri, koma anaphonya lumbiro la pangano.

⁶⁴⁶ Chomwechonso izo ziri lero. Munthu amapita ku tchalitchi, ndi kukajowina mipingo yayikulu, ndi kumayesera kuti akhale munthu wotchuka kwambiri mu mzinda. Ngati iwo akufuna kuti ajowine mpingo, iwo amapeza waukulu kwambiri mu mzinda, wopambana ndi woganiziridwa bwino mu mzinda. Momwe iwo amaphonyera maitanidwe! Momwe iwo amaphonyera Izo!

⁶⁴⁷ Njira yokhayo imene mungamudziwire Yesu Khristu ndi mwa vumbulutso lauzimu, osati mwa zaumulungu ndi kuchuluka kwa momwe mumaphunzirira Baibulo. Kaya ndinu wa Christian Science, Methodisti, Mboni za Yehova, kapena chirichonse chimene inu muli; ziribe kanthu chimene inu muli, inu simudzadziwa Izo mwa Mawu, ndi Mzimu wa Mulungu umene umamuulula Iye kwa inu. Ndi vumbulutso lauzimu!

⁶⁴⁸ Pamene Adamu, m'munda wa Edeni, ndi Eva, pamene ana amenewo anaponyedwa kunja, apa anabwera Kaini ndi zaumulungu zabwino. Iye anati, "Mulungu akuyenera kudziwa kuti ife tikuchita izi kuchokera mwa kupambana—kupambana kwa mtima wanga. Ine ndimanga guwa lokongola, ndiyika maluwa pa ilo, ndiyika zipatso pa ilo, ndilikongoletsa ilo. Ndithudi ndikhoza kumukondweretsa Mulungu ndi izi ndi kumudziwitsa Iye kuti ndine woona mtima mu mtima mwanga." Iye anali wolondola momwe Mawu ankapitira; Mulungu ankafuna kupembedza, iye anapita kukapembedza. Iye anapanga malo okongola oti azipembedzeramo, kafiduro wamkulu, wabwino (monga iwo amamutchulira iye lero). Ndipo anampanga iye bwino, anammanga iye molondola ndipo anaika guwa mmenemo; iye sanali wosakhulupirira.

⁶⁴⁹ Koma Abele, pa Mawu a Mulungu. . . Panalibe Baibulo lolembedwa nthawi imeneyo, koma Mulungu *anaulula* kwa iye kuti sichinali chipatso chimene chinatitulutsa ife m'munda wa Edeni, sanali maapulo amene Adamu ndi Eva anadya, izo zinali mwamtheradi zinthu zogonana zomwe zinawalekanitsa iwo ndi kuwagawaniza iwo. Ndipo podziwa kuti iwo anadzakhala achivundi, ndipo kudzera mu magazi a Adamu, ndi kudzera mu magazi a serpenti ndi zimene zinayambitsa izi, Abele, mwa vumbulutso Lauzimu, anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa ndipo anamupereka iye. Ndipo Mulungu anati, "Ndi Zimenezotu!" Ndithudi.

650 Pamene iwo anatsika kuchokera pa Phiri la Chiwalitsiro, Yesu anati, “Kodi munthu amanena kuti Ine Mwana wa munthu ndine yani?”

651 “Ena amati Ndinu ‘Mose,’ ndipo ena amati Ndinu ‘Eliya,’ ndipo ena amati Ndinu ‘Yeremiya,’ ndipo ena amati Ndinu ‘Mneneri ameneyo.’”

652 Iye anati, “Koma inu mukuti Ine ndi ndani?”

653 Petro anati, “Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu Wamoyo.”

654 Iye anati, “Wodala ndi iwe, Simoni Bar-yona, pakuti thupi ndi magazi sizinawululire izi kwa iwe.” (Penyani!) “Osatinso kudzera mu lemba, osatinso kudzera mu sukulu; iwe sunaphunzire izo mu seminare, ngakhalenso kuti winawake anakuuza iwe. Thupi ndi magazi sizinawululire izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awululira izo kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzakhoza kuwulaka Iwo.” Ndi zimenezotu pamenepo. Ndi umeneyo Mpingo wa Mulungu wamoyo. Ndi zimenezotu. Pa mpingo umenewo. . . Pa *vumbulutso* limenelo, Mpingo uwu wamangidwapo. Ndi vumbulutso Lauzimu kuti Mulungu wawulula, kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo inu mwamulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu wanu, mwadutsa kuchoka ku imfa mwapita ku Moyo.

655 Ndipo Mzimu Woyera ukuyenda ndipo ukugwira ntchito mwa ziwalo za Thupi ili. Ndi umenewo Mpingo! Ziribe kanthu ngati iwo uli wosauka, ndi mu mishoni, ndipo inu nkukaima panso pa mtengo wa paini penapake, kapena kulikonse kumene uko kuli, ngati ziri mnyumba ya winawake mu msonkhano wamseri, ziribe kanthu kumene iwo ukanakhala. Kukongola ndi zinthu sizimamupepetula Mulungu. Ndi kuwonantima kwa mtima mwa vumbulutso kuti Yesu Khristu waperekedwa ngati Mwana wa Mulungu, Mpulumutsi wathu wathu. Amen!

656 Mai, ife. . . inu simumazipeza izi, kudzera monga choncho, ife tingatero?

657 Awo ndi amene. . . uko kumene Iye anapita; angelo: amithenga, alaliki amenewo, aluntha amenewo, amithenga amenewo amene sanakhulupirire pamene Nowa anapita kukalalikira kwa iwo ndipo anawauza iwo, “Bwanji, mukudzalowa mchombo ichi.”

658 Iwo anati, “Tamumvereni woyera wodzigudubuza uyu. Tamumvereni wotengeka ameneyo. Bwanji, kulibeko mvula. Ndani anayamba wamvapo za chinthu choterocho? Bwanji, mai, ife tiribe mipingo? Kodi ife si achipembedzo?” Bwanji, iwo anali achipembedzo!

659 Yesu ananena kuti iko kadzakhala kam’badwo kamene kanadutsa nthawi imeneyo, kakanadzakhala kam’badwo kameneko kamene kakanadzabwerezanso Kudza Kwake

kusanachitike, “Monga mmene zinali m’masiku a Nowa, chomwechonso kudzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu. Pakuti iwo ankadya, kumwa, kukwatira, kukwatiwa.” Iwo anali ndi Reno, Nevada nthawi imeneyo, kwinakwake. Iwo anali ndi mitundu yonse ya zamkutu zimene iwo ali nazo lero; kupikisana, ndi kusewera, ndi kusekana, onyoza ndi zina zotero; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Choonadi chenicheni: pangano, Uthenga wa chisomo. Mulungu akupanga njira Yake, ndi kuwapatsa anthu Lake—pangano Lake, momwe angathawire; Iwo unali ndi chipulumutso mmenemo, chipulumutso chinali malo othawirapo.

⁶⁶⁰ “Kodi ife tikusowa chiyani ndi chipulumutso?” Lero anthu amati, “Kodi ife sitikukhala pansu pa boma labwino la demokalase? Kodi ife tikusowa chiyani?”

⁶⁶¹ Ine sindikusamala kuchuluka kwa boma la demokalase limene tikukhalamo, ife tikusowa Magazi a Yesu Khristu. Kulondola! Ife tikumusowa Khristu. Ine ndimayamikira boma la demokalase; izo ziribe kanthu kochita ndi chipulumutso cha moyo. Mwamtheradi! Maboma amenewo adzapita, ndipo fuko lililonse lidzapita. Ndipo ine ndinayimapo pamene . . . pamene farao anayima, ndipo iwe umayenera kukumba mapazi twente pansu pa nthaka kuti upeze mipando yachifumu yawo pomwe iyo inkakhala. Afarao onse ndi maufumu ake a dziko lapansi, ndi zofooka zake zonse zidzalephera ndipo zidzachoka, koma Yehova adzalamulira kosatha, pakuti Iye ndi Mulungu wachisavundi. Mokhazikika pa Thanthwe Khristu Yesu ife tayima, pakuti maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

⁶⁶² Kusamala ngati izo . . . maufumu adzawuka ndi kulephera, koma, oh, palibe kalikonse, ine sindikusamala kaya icho ndi chirichonse, palibe chomwe chiripo, palibe chamtsogolo, palibe (njala kapena zowopsya kapena chirichonse) chingakhoze konse kutilekanitsa ife ku chikondi icho cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu. Pamene munthu abadwa mwa Mzimu wa Mulungu, iye sakhalanso cholengedwa cha nthawi, koma iye ndi cholengedwa cha Muyaya. Ameni. Iye wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Iye wadutsa kuchokera ku . . . Iye wadutsa mu gawo la nthawi, wadzalowa mu Muyaya. Iye sangawonongeke konse! Ndipo Mulungu analumbira kuti Iye adzamuukitsa iye mmasiku otsiriza.

⁶⁶³ Chotero iwo akhoza kukhala ndi mipingo yanu yonse yayikulu, ndi nthawi zanu zonse zazikulu, ndi zonse zomwe inu mukuzifuna, ndi kunena nthabwala zanu zonyansa ndi kukhala ndi masewera anu a Bunco, ndi mgonero wa supu ndi china chirichonse chimene inu mukufuna kutero; ndi kukhala ndi mlaliki wina wophunzira atayima pamenepo. Mwinamwake iye akhoza kuchita ntchito yabwinoko kuposa ena a anyamata aang’ono awa amene samadziwa nkomwe ma ABC awo. Koma ine ndikukuuzani inu choonadi, ine kulibwino ndikhale ndi

mnyamata yemwe samadziwa ABC wake akulalikira kwa ine (amene amamudziwa Khristu) kuposa azaumulungu onse aakulu amene alipo ndi maphunziro anu onse omwe angaganiziridwe. Mwamtheradi!

⁶⁶⁴ Kumusi kuno mu Kentucky, osati kale kwambiri, mnyamata wachikulire amene sankakhoza nkomwe kuwerenga dzina lake lomwe, anati Ambuye anamuyitana kuti azilalikira ndipo iye ankafuna nyumba ya sukulu. Bwanji, a malamulo sanamulole iye kuti ayitenge iyo. Mlaliki wina wamkulu anabwera kumeneko ndi chogwirira pa dzina lake monga *choncho*, dokotala wina wamkulu wa zaumulungu, bwanji, iwo anamulola iye atenge sukuluyo. Ndithudi. Anakhala ndi chitsitsimutso cha masabata awiri, popanda moyo umodzi. Ndipo abambo ake anabwerera, anati, “Tsopano inu mumulole iye atenge iyo, ndine wolipira msonkho, ine ndiri ndi ufulu kuti mwana wanga atenge iyo. Ndipo mwana wanga akuyenera kutenga iyo nayenso.”

⁶⁶⁵ Chotero iye anabwerera kuti akafufuze, ndipo anawafunsa iwo, iwo anati, “Chabwino, ife timulola iye kuti atenge iyo osachepera mausiku awiri.” Ndipo iwo anapitirira ndipo anamulola iye kuti atenge iyo mausiku awiri.

⁶⁶⁶ Ndipo usiku umenewo mnyamata wachikulire wamng’ono yo anapita kumeneko ndipo samatha nkomwe kuwerenga Baibulo, anali ndi winawake woti amuwerenge mutu wake. Koma pamene iye anayenda kupita pa nsanja, iye anadzedwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo pamene analalikira, pafupifupi twente anabwera ku guwa; ndipo mlaliki wodzitcha yekha uja analira njira yake mpaka ku Kalvare, pa guwa.

⁶⁶⁷ Ndithudi, m’bale, izo sindizo—si zimene inu mukuzidziwa, ndi Amene inu mukumudziwa. Ndiro lingaliro lake, izo ndi zomwe zimatengera, zimatengera kumudziwa Khristu. Kumudziwa Iye, ndi Moyo; kumukana Iye, ndi imfa.

⁶⁶⁸ Mwamsanga ku mafunso athu ena, mafunso tsopano amene akupita ku Georgia:

67. Kodi miyala mu...imaimira chiyani mu Chivumbulutso 21:19 ndi 20?

⁶⁶⁹ Ngati mukufuna kutenga nthawi kuti mutsegule Mabaibulo anu, zomwe ife tiribe nthawi yochuluka tsopano, koma ndiyetsa kuwayankha iwo mwaliwiro. Chivumbulutso twente-...Ine ndikukhulupirira kuti ndi 21:19 ndi 20. Inde.

⁶⁷⁰ Chabwino, mmenemo inu mupeza kuti iye ankayankhula za miyala imene inali mnyumba. Ndipo miyalayo inali maziko. Ngati inu mungazindikire...Ine ndikukhulupirira inu muli nazo izo pamenepo, M’bale Neville. Ndipo mwala uliwonse unali maziko. Osati mwala umodzi maziko, ndi inayo... Koma mwala uliwonse unali maziko. Mwala uliwonse unali maziko osalekeza. Ndipo panali miyala thwelovu. Ndipo ngati mungazindikire miyala thwelovu imeneyo, upatseni uliwonse...

Choyamba kuyambira ndi yaspi, ndi sardiyo, ndi ina yotero monga choncho, kuyimira mwala uliwonse.

671 Mu Baibulo mupeza kuti iyo inkatchedwa miyala inayake. Ina ya iyo yosiyana pang'ono, inu simunamvepo za iyo. Ngati mungayang'ane mmbuyo mu dikishonare mupeza kuti ndi mwala womwewo, dzina losiyana basi; lasinthidwa.

672 Koma izo zikuyamba ndi—ndi yaspi. Yaspi unali mwala wa—wa Benjamini, kapena, mwala wa . . . oh, mwana woyamba, Rubeni. Mwala woyamba unali Rubeni, umene unali yaspi. Mwala womalizira unali Benjamini, mwala womalizira pamwamba.

673 Tsopano, miyala thwelovu iyi imene maziko anayikidwapo, iyo—miyala thwelovu imeneyo imapachikidwa pa chapachifuwa cha Aroni. Ndipo iwo—iwo ankaimira, iye anali mkulu wa ansembe wa—wa mafuko awa. Uliwonse wa mwala wawo wakubadwa mkati umu, mu iyi—mbale iyi. Ndipo pamene anthu awona mbale iyi, iwo amazindikira kuti Aroni anali mkulu wa ansembe wa fuko lonselo, pamene iwo anawona mwala wakubadwa m'mbale iyi.

674 Tsopano, pamene ife tinafika mmawa uno mu uthenga wa M'bale Neville. Ndipo nthawi zambiri zimene abweretsa Urimu Tumimu. Inu mumawona izo zimatchulidwa mu Baibulo monga njira imene iwo ankadziwira ngati uthenga wawo unali Choonadi kapena ayi. Miyala imeneyo, pamene iwo ankapita kukanena zomwe munthuyo ananena, mneneri ankalosera, ndipo miyala imeneyo yonse inkanyezimira palimodzi. Iyo inkapanga kuwundana kwa kuwala kumene kunkawoneka ngati safire, ndi yaspi, ndi kalabankulo, ndi miyala ina yonseyo ikunyezimiritsa kuwala kwawo, iyo inkapanga mtundu umodzi waukulu kwambiri wokongola wa utawaleza umene unkasakaniza chinthu chonsecho pamodzi.

675 Tsopano, tsopano, lero, pamene Urimu Tumimu uja anachotsedwa ndi unsembe umenewo, tsopano Baibulo ili ndi Urimu Tumimu wa Mulungu lero. Ndipo pamene mlaliki alalikira, asamangokhala malo amodzi aang'ono okha apa, ndipo ndizo zonse zimene iye akuyikapo ziyembekezo zake; likuyenera kukhala Baibulo lonse likunyezimiritsa uthenga umene munthuyo akulalikira. Chimenecho ndicho chinthucho. Osati malo amodzi okha, ndikuti, “Chabwino, Baibulo limanena *izi*.” Oh, ndithudi, Ilo limanena zinthu zambiri. Koma inu mukuyenera kuzipanga zonsezo kuyikidwa pamodzi. Ndipo pamene Mzimu wa Mulungu ubwera ndi kudzalowa mu a—Mawu, Iwo umaziyika izo zonse pamodzi ndi kudzanyezimiritsa Kuwala kumodzi kwakukulu, ndipo Kuwala kumeneko ndi Yesu Khristu. Amen.

676 Tsopano, miyala thwelovu iyi inali maziko thwelovu amene anayamba kuchokera kwa Rubeni, ndi Gadi, ndi kumapitirira

mpaka kwa Benjamini; mafuko thwelowu, miyala thwelowu. Ndipo miyala imeneyo mu Kachisi, mu Yerusalemu watsopano wa Kumwamba, maziko aliwonse adzayikidwa pa mmodzi ya mbadwa.

⁶⁷⁷ Tsopano penyani, inu muzindikire miyala, tsopano inu muwona mbadwa zimenezo zikunyezimira mu chinachakenso, basi mu funso lina.

68. Tafotokozani—tafotokozani chachinayi...zirombo zinayi za Chivumbulutso 5.

⁶⁷⁸ M'bale Neville, ngati inu muli nazo izo pamenepo pafupi, kapena wina wa inu, za Chivumbulutso 5, ife tiweringa izi kwa miniti yokha. Ndi a—ndi chithunzi chokongola apa cha... Apa, ine ndiri nazo izo mwiniwanga, Chivumbulutso mutu wa 5:

Ndipo ndinawona mdzanja lamanja la iye amene anakhala pa—pa mpando wachifumu bukhu lolembedwa mkati ndi kunja ndi—ndi—ndi kuseri, losindikizidwa ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri.

Ndipo ine...

⁶⁷⁹ Tsopano, malo ake si amenewo. Ine ndikufuna kuti ndipite patsogolo pang'ono, zirombo zinayi. Tiyeni tiwone, ndime ya 14. Chabwino, bwana. Tsopano apa ife tikupita, ndiko kulondola. Tsopano tiyeni tiyambire apa pa—pa ndime ya 12, ayi, ine ndikuganiza... “Ndipo zirombo zinayi zinati, ‘Ameni.’” Ayi, pali malo aang'ono kuseri kwa izo, M'bale Neville. “Taonani, ine ndinamva liwu, ...”

⁶⁸⁰ Tiyeni tiwone, miniti yokha, ine ndimawerenga izo kanthawi kapitako. Oh, ife tiri pano, tiyeni tiyambire pa ndime ya 6. Ndime ya 5:

Ndipo mmodzi wa akulu anati kwa ine, Usalire ayi: taona, Mkango wa fuko la Yuda, Muzu wa Davide, walakika kutsegula bukhu, ndi kumasula... zisindikizo zake.

Ndipo ine ndinawona, ndipo, ... pakati pa mpando wachifumu ndipo... zirombo zinayi, ndi, pakati pa akulu, panayima Mwanawankhosa ngati, anali ataphedwa, wokhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi maso asanu ndi awiri, yomwe ili Mizimu isanu ndi iwiri... wotumizidwa kuchokera kwa... ku dziko lapansi.

⁶⁸¹ Ine ndikufuna inu mugwire funso limenelo, ndipo ngati ine sindilimvetsa ilo pansu apa mu miniti, ine ndikufuna kuti mudzalibweretsenso, ndikufuna kuti ndichite pa ilo, “Mizimu isanu ndi iwiri ya maso asanu ndi awiri amene anali pa Mwanawankhosa.” Oh, icho ndi chinthu chokongola kwenikweni. (Chabwino, ife tikufuna kuti titenge funso la m'bale uyu tsopano.) Chabwino, musaiwale izo tsopano.

Ndipo iye anabwera ndipo anatenga bukhu kuchokera mdzanja lamanja la iye wokhala pa mpandowachifumu.

Ndipo pamene iye analitenga ilo, zirombo zinayi ndi akulu foro ndi twente anagwa panso pamaso pa mwanawankhosa, . . . aliyense wa iwo ali ndi azeze, . . .

⁶⁸² Tsopano, ndizo—zinayi—zirombo zinayi apa, ngati inu mungazindikire. Tsopano tiyeni tipite patsogolo ndi kukawerenga patsogolo pang'ono:

. . . azeze agolide, . . . odzaza ndi mbale ndi zonunkhira, . . . ndi mapemphero a oyera mtima.

Ndipo iwo anayimba nyimbo yatsopano, . . . Ndinu woyenera. . . (ndipo anapita patsogolo ndi kupanga kwawo . . . kupembedza kwawo konse kwa Ambuye)

⁶⁸³ Tsopano, zirombo zinayi izi za Chivumbulutso, ngati inu mungazindikire izo, malo aliwonse. . . (Inu owerenga Baibulo, ndi anthu amene ati adzamvetsere ku kujambula kwa tepi iyi). Zamoyo zinayi zimenezo, zinali ndi nkhope zinayi: chimodzi chinali ndi nkhope ngati munthu, china chinali ndi nkhope ngati ng'ombe, ndipo nkhope ina inali ngati mphungu, ndipo nkhope ina inali ngati mkango. Ndipo izo sizinkabwerera mmbuyo, izo sizikanakhoza kupita mmbuyo.

⁶⁸⁴ Ndi angati amene akukumbukira bukhu lakale la Chivumbulutso pamene ankaliphunzitsa ilo zaka zapitazo, pamene ine ndinatenga pafupifupi zaka ziwiri pano pa Bukhu la Chivumbulutso? Ambiri akale akukumbukira.

⁶⁸⁵ Taonani, izo sizimabwerera mmbuyo, chifukwa mbali iliyonse yomwe izo zimapita zinkapita chitsogolo. Ngati izo zikupita mbali *iyi*, izo zinkapita ngati munthu; ngati zikupita mbali *iyi*, izo zinkapita ngati mkango; zikamapita mbali *iyi*, izo zinkapita ngati mphungu; ngati zikupita mbali *iyi*, izo zinkapita ngati ng'ombe. Mwaona, izo sizimabwerera chammbuyo, izo zinkapita chitsogolo nthawi zonse.

⁶⁸⁶ Tsopano zamoyo zinayi zimenezo. Tsopano kuti mumvetse izi mwamsanga, chifukwa sindikufuna kukhala motalika kwambiri pa izi. Koma zamoyo zinayi. . . *chamoyo*, mu Baibulo, chimaimira “mphanvu.” Ndipo inu mukuzindikira kuti zamoyo izi sizinali kutali uko mu nyanja kapena mu nyanja yayikulu kwinkakwake zikubwera, koma izo zinali Pampando wachifumu wa Mulungu, ndipo zinkamupembedza Mulungu. Zamoyo zinayi zimenezo zikutanthauza mphanvu zinayi zomwe zinabwera kuchokera pa dziko lapansi, ndipo mphanvu zinayi zimenezo zinali Mauthenga anayi: Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane; umodzi sumatsutsana ndi umzake.

⁶⁸⁷ Ndipo umodzi wa iwo, a . . . Pamene Uthenga ukupita ngati mkango, iwo ndi wamakani, ndi wolimba; Uthenga ndi wolimba mtima ngati mkango, ndipo ndi mfumu ngati mkango. Ngati iwo

umapita kuyandikira nkhope ya munthu, iwo ndi wochenjera ndi wothyathyalika monga munthu. Ngati iwo ukupita ngati mphungu, iwo umakhala ndi mapiko aliwiro ndi kumakwera mmwamba. Iwo... Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ngati iwo ukupita ngati ng'ombe, ndiye kavalo wantchito amene amatha kukoka, ng'ombe yantchito imene imakoka—a—katundu wa Uthenga. Zamoyo zinayizo zinali mphamvu zinayi, zomwe zinali: Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane; Mauthenga anayi amene amamveka mu Kukhalapo kwa Mulungu. Izo zinali. . .

⁶⁸⁸ Ngati inu munazindikira, izo zinali ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo. Izo—izo... Kulikonse kumene izo zinkapita, izo zinkanyezimiritsa. Izo zinkawona kulikonse kumene izo zinkapita. Ndipo imeneyo ndi mphamvu ya Mauthenga pamene iwo akutuluka, izo zikhoza... Izo ziri ndi kuthyathyalika kwa munthu; ziri ndi liwiro la mphungu; ziri ndi—ndi—ndi—mphamvu, mphamvu yokoka, wonyamula katundu ngati ng'ombe; izo ziri ndi—kulimba ndi kulimba mtima kwa mkango. Mwaona, ndi Mauthenga anayi, amene ali mphamvu zinayi za Chivumbulutso, mutu wa 4.

Chabwino, tsopano lotsatira:

69. Kodi akulu twente-foro ndi ndani? Chabwino, ine ndikukhulupirira izo zingakhale pa a—a... **Kodi akulu twente-foro ndi ndani?**

⁶⁸⁹ Tsopano ilo ndi lophweka basi, ife tikhoza kufika kwa ilo. Akulu twente-foro amakhala patsogolo pa Mpandowachifumu. Izo ndi mu... Ndikukhulupirira kuti izo ziri mu ndime 4, ndi pamene izo zikupezeka. “Ndipo apo panapita wina...” Ine ndikuyenera ku... Tiyeni tiwone, ine nda... 4:10.

⁶⁹⁰ Chabwino, Chivumbulutso, mutu wa 4, ndi ndime ya 10. Uko nkulondola. Ife tifika kwa izo.

Ndipo akulu twente-foro anagwa pansi pamaso pa iye wakukhala pa mpando wachifumu, ndipo anamupembedza iye wakukhala moyo ku nthawi za nthawi, ndipo anaponya nduwira zawo ku mpando wachifumu ndikuti,

Inu ndi woyenera, O Ambuye, kulandira ulemelero ndi ulemu ndi mphamvu: pakuti inu munalenga zinthu zonse, ndipo mwa kukondweretsedwa kwanu izo ziripo ndipo zinalengedwa.

⁶⁹¹ Tsopano akulu foro ndi twente. Mkulu ndi woyang'anira. Tsopano zindikirani, iwo anali mbadwa thwelovu ndi atumwi thwelovu. Ndipo iwo anali atakhala, thwelovu kumbali imodzi ndi thwelovu kwinkako. Panali akulu twente ndi foro, amene anali mbadwa thwelovu mbali imodzi, Chipangano Chakale, atumwi thwelovu mbali inayo, a Chipangano Chatsopano. Kodi Yesu sanati, “Inu mudzakhala pa mipandoyachifumu thwelovu, kuweruza mafuko thwelovu a Israeli?”

⁶⁹² Tsopano, maziko. Taonani, muli ngakhale mtengo mmenemo. Ndipo mtengo mbali zonsezo umabala mitundu thwelovu ya zipatso. Ndipo iyo imabala zipatso zawo kamodzi pamwezi, imene ili miyezi thwelovu mu chaka. Iyo imapereka mitundu thwelovu ya zipatso chaka chirichonse pamene icho chikupita. *Thwelovu* ndi nambala ya “kupembedza” ija, inu mwaona. Ndipo pali twente ndi foro, akanakhala twente-foro, atumwi thwelovu ndi mbadwa thwelovu. Iwo akhala pa Mpandowachifumu.

⁶⁹³ Chabwino, tsopano ndime ya 4, kapena, funso lachinayi:

70. Kodi chingwe chofiira mu Genesis 38 chinkaimira chiyani?

⁶⁹⁴ Chingwe chofiira, ngati inu mungazindikire, anali Yuda. Ndipo iye anali ndi ana aamuna, ndipo mmodzi wa ana ake anakwatira mkazi wa ku Kanani. Ndipo mkazi Wachikanani uyu analibe mwana aliyense, ndipo mwana wake wamwamuna anamwalira. Kenako, lamulo ndiye linali loti atenge...mwana wotsatira ankayenera kutenga mkazi wa m'bale wakeyo, ndi kuwukitsa mbewu kwa wakufayo. Ndipo munthu winayo sanagwirizane nazo ndi kuchita mmene iye ankayenera kuchitira, ndipo Ambuye anamupha iye. Ndiye iye anali ndi mwana wamwamuna wamng'ono; chotero Yuda anati, “Udikire mpaka mwana uyu adzayendetse...adzakule mpaka kufika pa malo amene iwe ungakwatiwe naye.”

⁶⁹⁵ Ndipo pamene iye anakula kufika pamalo pomwe ankayenera kukwatira mkazi wakale wa abale ake awiri, chabwino, iye ankayenera kuti amutenge iye ndiye, kuti awukitse mbewu kwa abale ake omwe anali...amene anali atamwalira iye asanabwere. Yuda sanampatse mkaziyo (mkazi wa ku Kanani) mwana wamwamuna, mnyamata, ndipo anangomusiya iye kuti azipita. Chotero iye anawona kuti iye amalakwitsa, chotero iye anatuluka ndipo anakakulunga chophimba pa nkhope yake, ndipo anakakhala pa malo owonekera monga hule angakhalire.

⁶⁹⁶ Yuda anabwera apo ndipo anamutenga mkaziyo ngati mkazi wake, ndipo iye anali hule, ndipo anagona naye iye. Ndipo anati, iye anati, “Chabwino, ungalonjeze chiyani ndi ine?” Ndipo iye... iye anati...

⁶⁹⁷ Iye anati, “Ine ndimupatsa iye a—mwana.” Iye anati, “Chabwino, ndipatse ine chizindikiro kuti uchita izo.” Chotero iye anatenga ndodo yake ndi chosindikizira chake ndi zina zotero, ndipo anazisunga izo.

⁶⁹⁸ Ndipo pamene iwo anamubweretsa mwanayo, iwo sanamupeze huleyo, chifukwa iye sanali hule.

⁶⁹⁹ Patapita kanthawi, iye anawonekera kuti iye anali woti akhale mayi. Ndipo pamene iye anawonekera kuti iye anali woti akhale mayi, iwo anabwera kudzamuuza Yuda, “Mpongozi wako

wachita gawo la hule.” Anati, “Chifukwa chakuti iye—iye ndi woti akhala mayi, ndipo anyamata ako onse anamwalira.”

⁷⁰⁰ Iye anati, “Chabwino, iye ayitanidwe, ndipo mumuwotche iye.”

⁷⁰¹ Ndipo chotero iye anatomiza mawu kwa Yuda, ndipo iye anati, “Munthu amene wachita izi, ndi mwini wa ndodo iyi ndi chosindikizira ichi.” Chabwino, amenewo anali apongozi ake aamuna.

⁷⁰² Ndipo iye anati, “Iye ndi wolungama kwambiri kundiposa ine.”

⁷⁰³ Tsopano, pamene anadziwa kuti ana ake anali oti abadwe, iwo anali amapasa. Ndipo pamene mapasasa . . . Mwana woyamba amene anali woti abadwe, mwambo wakale Wachiyuda, mwana woyamba amakhala ndi ukulu wa kubadwa, mwana woyamba kubadwa. Ndipo ameneyo, kumbukirani, anali mwana wake woyamba. Palibe aliyense wa anyamatawo amene anali ndi mwana mwa iye. Iye anali asanakhalepo ndi mwana mpaka nthawi iyi.

⁷⁰⁴ Ndipo pamene mwana wake woyamba anatulukira, iwo unangokhala nkono. Ndipo namwino anayika chingwe chofiira mozungulira iwo, chifukwa chingwe chofiira chinkayankhula za chiwombolo kuti mwana woyamba wa namwali Mariya akanadzakhala . . . adzakhala ndi chingwe chofiira cha chiwombolo.

⁷⁰⁵ Ndipo pamene iye anabweza dzanja lake mmbuyo, winayo anabwera poyamba. Ndipo pamene iye anatero, anati, “Chifukwa chiyani iwe wachita izi? Winayo ali ndi ufulu wakubadwa.”

⁷⁰⁶ Kotero ndicho chimene Genesis 38 akutanthauza, inu mwaona, kuti mwana woyamba anakhalabe kufikira kudza kwa Ambuye Yesu Khristu, kuti woyamba anali pansu pa lamulo la chiwombolo.

⁷⁰⁷ Inu mukudziwa ine ndinati . . . bulu wamng’ono, inu mukudziwa, ine ndinakambapo za iye, kuti maso ake anali . . . chirichonsecho, makutu ake ogwera pansu, koma, ngati iye anabadwa ali ndi ufulu wakubadwa, mwanawankhosa wosalakwa, wangwiro anafa mmalo mwake. Ndi zimenezotu.

⁷⁰⁸ Chotero izo zinali za ufulu wakubadwa. Mwana woyamba amene anatuluka kuchokera kwa amayi, ndipo iwo analiwona dzanja limenelo (ndipo anadziwa kuti ilo likhoza kubwereranso kachiwiri). Ndipo pamene iye anakankha dzanja lake kuti awonetse kuti anali nalo, iye anali woyamba, mzamba anamanga chingwe chofiira mozungulira ilo ndipo iye anabweza dzanja lake mmbuyo. Mukuona? Koma, mwamtheradi, iye anali woyamba. Chimenecho chinali chingwe chofiira, chingwe chofiira cha . . . njira yonse kudutsa mu Baibulo, icho

chimatanthauza chiwombolo; chimene chinkalozera mtsogolo kwa mwana woyamba kubwera.

⁷⁰⁹ Kavalo woyamba kubadwa, ng’ombe yoyamba kubadwa, chirichonse chimene icho chinali, chirichonse chimene chinabadwa koyamba (chimene chinatulukira) chinali pansu pa chiwombolo, chinkayenera kuwomboledwa; chirichonse chinkayenera kuwomboledwa! Aleluya! Oh, izo zikungondikondoweza ine. Kodi inu mukumvetsa zimenezo? *Woyamba* ankayenera kuwomboledwa. Ilo linali lamulo. Lidalitsike Dzina la Ambuye!

⁷¹⁰ Ndipo pamene Yesu Khristu anabadwa, Iye anawombola dziko lonse. Ndithudi, Iye anatero. Iye anali Muwomboli wa cholengedwa chirichonse chimene chinalengedwapo pa dziko lapansi. Iye anali Muwomboli. Ndipo pa . . .chiwombolo chonse chiri mwa Iye, ndipo palibe njira ina nkomwe imene inu mungabwerere mwa ntchito zabwino, pa kujowina mpingo, kapena chirichonse chimene icho chiri; inu mukuyenera kubwera ndi chingwe chofiira chimenecho, Muwomboli ameneyo, Wowombola wachibale ameneyo.

Chabwino, tsopano lotsatira ndi:

71. Ziri kuti mphatso...Kodi mphatso zake ndi ziti zimene zidzatumizidwe pa imfa ya mboni ziwiri za pa Chivumbulutso 11?

Oh, M’bale Palmer, ngati inu simungafunse mafunso ena!

⁷¹¹ Tsopano, chiwombolo, zingwe izi apa, chingwe chofiira ichi, ife tikuwona icho chinkatanthauza chiwombolo.

⁷¹² Tsopano funso lotsatira ndi:

Kodi mphatsozo ndi ziti mu Chivumbulutso 11?

⁷¹³ Ikubwera nthawi. . .Tsopano apa tiyankha funso limene linayankhidwa usiku wina, limene mlaliki mzanga analemba za Ayuda, momwe izo zidzakhaliwe.

⁷¹⁴ Tsopano Ayuda awa ali ndi zaka zitatu ndi theka zolonjezedwa kwa iwo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Masabata sevente analonjezedwa. Anati, “Mesiya adzabwera ndipo adzadulidwa mkati.” Zaka zitatu ndi theka Khristu analalikira, anaphedwa mu zaka zitatu ndi theka ndendende, zaka zitatu ndi miyezi sikisi Iye analalikira.

⁷¹⁵ Ndi kenako chonyansa chopangitsa chipululuso, a—msilamu waku Omar unaikidwa pa Nthaka Yoyera; monga Mulungu ananenera, zaka twente-faivi handiredi izo zisanachitike, iwo ukanadzakhala uli pamenepo. Mneneri anawuwona iwo, ndipo anawuwona iwo, ndipo anati iwo akanadzatero, Amitundu, akanadzakhala eni ake kumeneko mpaka nyengo ya Amitundu itatha.

⁷¹⁶ Tsopano pali zaka zitatu ndi theka zolonjewedwa. Ngati inu mungazindikire, mboni izi za Chivumbulutso 11 zimalosera masiku sauzande, thuu handiredede ndi sikisite; ndendende zaka zitatu ndi theka. Tsopano... ndipo iwo anali atavala ziguduli. Tsopano, penyani utumiki wawo, chimene iwo ali. Tsopano, mboni ziwiri izi zaphedwa.

⁷¹⁷ Tsopano, a... Iwo anabwerera kwa Ayuda utachitika Mkwatulo wa Mpingo wa Amitundu. Mpingo wa Amitundu ukupita Kwawo ku Mgonero wa Chikwati, ndipo monga Rebekah anatengedwera ku malo a Abrahamu limodzi ndi Isaki ndipo kumeneko anakakwatiwa. Ndipo Rebekah ndi Isaki anatulukako ali ndi zonse zomwe Abrahamu anali nazo, zonsezo zinapita kwa Isaki. Mwamtheradi! Ndipo izo sizikanabwera kwa Isaki mpaka Isaki atakwatiwa atakwatira. Oh aleluya! Ndi zimenezo pamene.

⁷¹⁸ Ndipo Khristu akudzakhala... Mulungu akudzakhala mu thupi lowonongedwa langwiro limenelo, kwathunthu kwa nthawizonse ndi kudutsa Muyaya. Pamene Mwanawankhosa ndi Mkwatibwi akwatirana Kumwamba, Iye akuyenda mu umwini wathunthu. Mwamtheradi! Isaki ndi Rebekah anabwera ali ndi umwini wathunthu.

⁷¹⁹ Ndipo pamene mwambo uwu ukuchitika Kumwamba, wa Mkwatibwi, Mkwatibwi wa Amitundu akukwatiwa kwa Kalonga (Mwana wa Mulungu), mu Ulemelero; pamene iwo akukwatirana, pali zaka zitatu ndi theka zimene zikuchitika pamene... Mose ndi Eliya...

⁷²⁰ Chimene, Mose sanasoweko nkomwe... ayi, thupi lake linanyamulidwa. Angelo anamutenga iye, iye sanavunde, iye sanawonongeke. Iye anali choyimira changwiro cha Khristu. Iye anafa ndipo Angelo anamunyamula iye, ndipo ngakhale mdierekezi samadziwa nkomwe kumene iye anayikidwa, ndipo anayesera kutsutsana ndi Mikaeli Mngelo wamkulu za kumene anakaikidwa. Ndicho chimene Baibulo linanena. Mulungu anamutengera iye mmwamba mu Mkwatulo.

⁷²¹ Ndipo Eliya, pamene iye ankayenda kumeneko, mneneri wa Mulungu, anayenda kupita ku Yordano, anavula chovala chake ndipo anamenyetsa madzi, ndipo iwo analekana kumanja ndi kumanzere. Iye anayenda chokwera mmwamba pa phiri. Elisha anati... Anati, "Two ukunditsatira ine chifukwa chiyani?"

⁷²² Iye anati, "Ndikufuna magawo awiri a Mzimu wanu."

⁷²³ Anati, "Iwe wapempha chinthu chovuta, koma ngati iwe udzandiwona ine ndikamapita." Iye anayika maso ake pa iye.

⁷²⁴ Ndipo patapita kanthawi, kutsika kuchokera Kumwamba kunadza galeta la moto ndi Angelo a moto, akavalo a moto, ndipo Eliya anakwera ndipo anapita mmwamba ku Ulemelero. Iye sanalawe konse imfa, iye anasinthidwa, iye akuyenera kuti adzafe!

⁷²⁵ Ndipo ngati inu mungayang'ane aneneri awiri awa a Chivumbulutso 11, iwo akuchita chinthu chomwecho chimene Mose ndi Eliya anachita. Inu mukuti, “M'bale Branham, kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti Eliya ndi Mose akadali moyo?” Mwamtheradi!

⁷²⁶ Bwanji, pamaso pa Phiri la Chiwalitsiro... Pa Phiri la Chiwalitsiro, Yesu asanapite ku Kalvare, pamenepo panayima awiri onse Mose ndi Eliya atayima pamenepo akuyankhula kwa Iye. Ndithudi, iwo anatero, iwo sanafe. Ndipo iwo anali asanafe konse; iwo ndi achivundi, iwo akuyenera kuti adzafe. Chotero iwo ali mu chikhalidwe chaulemelo basi akuyembekezera nthawi imeneyo.

⁷²⁷ Ndipo kenako pamene iwo adzabwerera ndi kudzalalikira ndendende zaka zitatu ndi theka pansi pa kudzoza kwa Ubatizo wa Mzimu Woyera, pamene madalitso achotsedwa kwa Amitundu (ndipo Mpingo watengedwera mmwamba); ndipo mpingo wozizira, wofunda uzidasakidwa ngati agalu, ndi chipani cha chikominisi ndi Chiroma, ndipo pamene iwo azidasakidwa ndi kumaphedwa. Iwo—iwo azidzaphedwa pamenepo; aneneri awa adzalalikira zaka zitatu ndi theka, ndipo Baibulo linanena kuti iwo anaphedwa mwa opambana... mu msewu, wotchedwa mwauzimu, Sodomu ndi Igupto, kumene Ambuye wathu anapachikidwa. Ndiko ku Yerusalemu; mwaona, mmbuyo mu Yerusalemu, wotchedwa mwauzimu.

⁷²⁸ Ndipo anakhala pa msewu kwa masiku atatu ndi usiku. Ndiyeno pamapeto a masiku atatu ndi theka, mzimu wa moyo udzabwerera mwa iwo ndipo iwo anawuka. Iwo ankayenera kufa monga anthu ena achivundi, iwo ankayenera kuti adzachite zimenezo. Ndipo pamene anawapha alaliki awiri awa...

⁷²⁹ Iwo analalikira motsutsa zoyipa, ndipo anabweretsa moto kuchokera kumwamba. Ndani anachita zimenezo? Mukuona? Iwo anabweretsa miliri kuchokera kumwamba, ndipo anakantha dziko lapansi mofulumira ngati... ndipo pa nthawi iliyonse imene iwo ankafuna kutero. Ndipo anatulutsa moto kuchokera kumwamba. Ndipo anaimitsa miyamba kuti mvula isagwenso, motalika momwe iwo ankafunira. Anali ndani ameneyo? Ndendende Mose ndi Eliya. Ndipo ndi zimenezo mboni ziwirizo.

⁷³⁰ Ndipo pamene iwo anawuzunza mpingo, kapena dziko, ndi kulalikira kwawo, ndi kuwalandiranso Ayuda, ndi kuwabwezeretsa iwo ku kulapa, kuwabwezeretsa iwo kuti akhulupirirebe... Pamene iwo adzamuwona Yesu akubwerera Mkwatibwi, iwo adzati, “Taonani, uyu ndi Mulungu wathu Amene ife tinkamuyembekezera. Ndi Iyeyo!” Koma Iye sakubwerera iwo; iye anabwerera Mkwatibwi Wake. Ndipo Mkwatibwi Wake...

⁷³¹ Pamene Yosefe anapita ku Igupto, iye sanawatenge abale ake pamodzi ndi iye, koma iye anakamutengera mkwatibwi wake

kumeneko. Mwamtheradi! Koma pamene anazidzindikiritsa yekha kwa abale ake, apo panalibe aliyense. Ndiko kulondola ndendende. Ndipo pamene Iye akuzidziwitsa Yekha kwa Ayuda awa, sipadzakhala aliyense kumeneko koma Ayuda. Ndi iwo amene anamupha Yosefe, atayima pamenepo; ndipo anati, “Chabwino, ndine Yosefe, m’bale wanu.” Ndipo iye analira.

⁷³² Ndipo iwo anati, “Tsopano ife tikudziwa kuti tiri mu izo, chifukwa ife tinamupha iye.”

⁷³³ Chinthu chomwecho, Ayuda amenewo adzakhala ndi nthawi yayikulu ija ya vuto kudza kusanachitike tsopano, ya chizunzo kuwathamangitsira iwo kubwerera ku dziko la kwawo. Izo zimawakusa iwo ngati gulu la nkhusa kubwerera ku Phiri la Karimeli kutaliko.

⁷³⁴ Pamene Ambuye Yesu adzabwerera Mkwatibwi Wake, ndipo iwo akadzamuwona Iye, iwo adzati, “Ameneyo ndi Amene ife takhala tikumuyembekezera, ndi Uyo apo!” Iye adzauka ndi machiritso mmapiko Ake. Uko nkulondola.

⁷³⁵ Ndipo mpingo, wotsalira wa Ayuda, pamene iwo potsiriza adzapha aneneri awiri awa, ndipo iwo nkudzagona mu msewu wotchedwa mwauzimu Sodomu ndi Igupto, kumene Ambuye wathu anapachikidwako, iwo adzatumizirana mphatso wina ndi mzake (dziko limatero).

⁷³⁶ Tsopano, M’bale Palmer, ndi inu apa. Muyang’ane mmbuyo mu mbiriyakale ya Chiroma ndipo mudzapeza kuti kuli fuko limodzi lokha mu dziko lonse limene linkatumiza mphatso nkondo ikatha, umenewo ndi Ufumu wa Chiroma.

⁷³⁷ Ndi chifukwa chake ine ndimanena kuti wotsutsakhristu akuchokera ku Rome. Chirombo chimachokera ku Rome, icho sichingatuluke kuchokera ku Moscow. Icho chimachokera ku Rome, chinjoka chofiira chimene chinayima pa mkazi kuti chimulikhwire Mwana wake mwamsanga pamene Iye anabadwa. Mdierekezi ameneyo, mdierekezi ameneyo anali kuti? Iye anali ndani? Kaisara Augustus yemwe anatumiza ndi kupha ana onse kuyambira usinkhu wa zaka ziwiri kutsika mmusi. Chinjoka chofiira, chinjoka, *chirombo* chimatanthauza “mphamvu.” Mphamvu ya Chiroma inazuna ndi kuyesera kuti amupeze Khristu Mwanayo.

⁷³⁸ Ndipo chinthu chomwecho! Nthawi iliyonse imene Aroma, Aroma achikunja akale ankakhala ndi chigonjetso chachikulu, iwo ankatumiza miyala yoyera ndi chirichonse kwa wina ndi mzake, ngati mphatso monga choncho, ngati zikumbutso. Chotero miyala imeneyo imene inali . . . Chimene iyo inali, inali mphatso zazing’ono zotumizidwa pakati pa mpingo wa Chiroma. Mwamtheradi! Ndendende. Izo zikuyenera kukhala.

⁷³⁹ Ine ndinayima pamenepo mu Mzinda wa Vatican ndi kutsimikizira izo ndi Baibulo. Papa atavala korona wapapatu, *Vicarius Filii Dei*, zinthu zonsezo zimene ine ndazimva ndi zina

zotero, izo ndi mwamtheradi ndi zoon; gulu lachipembedzo limene limalamulira fuko lirilonse pansu pa Kumwamba, ndipo ilo limatero. Ndi limenelo, ziri chomwecho.

⁷⁴⁰ Palibe chotsutsa anthu Achikatolika (ayi, bwana), iwo ndi abwino basi monga wina aliyense, koma chipembedzo chawo ndi cholakwika molingana ndi Baibulo ili. Ngati Baibulo ili likulondola, iwo akulakwitsa. Iwo amati iwo sama... “Ziribe kanthu zomwe Baibulo limanena, ndi zimene mpingo umanena.” Ife timakhulupirira kuti Baibulo limalankhula ndi ulamuliro wapamwamba! Mwamtheradi, ndi Mawu a Mulungu.

⁷⁴¹ Chotero inu mukuona pamenepo, miyala iyi imene inatumizidwa pamenepo, ya Vumbulutso apa, ndi—miyala imene inali mphatso yotumizidwa kwa wina ndi mzake. Zomwe zikungowonetsa... Baibulo linati, Vumbulutso apa, linati, “Mulole iye amene ali ndi nzeru awerenge chiwerengero cha chirombo. Mulole iye amene ali ndi nzeru achite *chakuti-ndi-chakuti*. Mulole iye amene ali ndi mzimu wa mphatso zina achite *chakuti-ndi-chakuti*.” Inu mukuona momwe mpingo uliri waufupi?

⁷⁴² Mnyamata wina anandifunsa ine mmawa uno za mphatso zauzimu, za kulankhula ndi malirime. Mnyamata wamng’ono, wodzipereka kwambiri, ine ndikukhulupirira iye adzakhala mtumiki ena a masiku awa. Ndipo za mpingo, ine ndinati, “Ziripo zochuluka za izo zomwe ziri zathupi. Ife sitikufuna zimenezo, koma tikufuna chinthu chenicheni. Ife tikulakalaka titakhala nazo.”

⁷⁴³ Inu simungapite kumakaphunzitsa izo mu tchalitchi; chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mumapeza, wina amakhala ndi lirime, wina amakhala ndi salmo, kenako inu mumayenera kulimbana nacho chinthucho. Koma pamene Mulungu wapereka mphatso mwayekha, iyo imadziwonetsera yokha. Ndiko kulondola. Mwaona, zimenezo ndi mphatso za Mulungu, izo ndi zimene Iye amazitumiza kwa Mpingo kuti ukagonjetsere.

⁷⁴⁴ Tsapano, wotsutsakhristu ali ndi chinachake monga ubwino ndi kuyipa kwake, iye ali ndi—a—njira yopotozedwa yochitira izo. Ndipo uwo ndi ufumu wa Chiroma umene ukutumizirana mphatso wina ndi mzake, mphatso zathupi. Mulungu amatumiza mphatso zauzimu kwa ogonjetsa; Aroma amatumiza mphatso zathupi kwa wina ndi mzake.

⁷⁴⁵ Ife timakhulupirira kuti Mzimu Woyera ndi Mzimu, ife timawulandira Iwo mwa ubatizo umene umachokera Kumwamba.

⁷⁴⁶ Mpingo wa Katolika umaphunzitsa, “Ukalisitiya woyera umene uli thupi la Khristu; kuti pamene mulandira mkate uwu ndi kokulumunya, izo *ndi* Mzimu Woyera, Mzimu Woyera, ukalistiya woyera.” Mukuona?

⁷⁴⁷ Ife timakhulupirira kuti ndi chidutswa cha mkate, sitimakhulupirira kuti ndi thupi la Khristu, (ife tikukonzekera kuti titenge iwo mu maminiti pang’ono). Ife timakhulupirira kuti iwo umayimira thupi la Khristu. Koma iwo sindiwo. . .

⁷⁴⁸ Ndiko kusiyana kwa pakati pa chiphunzitso cha Chikatolika ndi Chiprotestanti. Mukuona? Mpingo wa Katolika umati, “Thupi ndi. . . Mkate *ndi* thupi lenilenilo. Mpingo uli ndi mphamvu yosintha izi.” Kodi inu munayamba mwamuwonapo Mkatolika akamadutsa pa tchalitchi, amaweramitsa mutu wake, akupanga mitanda? Ndipo chifukwa kuwala kwakung’ono kuja kukuyaka mu tchalitchi umo pansu pa kachisi wamng’ono uyo. Muli kuwala pang’ono mmenemo, ndipo mkate wopatulika umenewo umakhala mmenemo. “Ndipo ndiro thupi la Khristu. Ndipo pamene inu mutenga izo, inu mwamtheradi mukutenga thupi lenileni la Khristu pa mgonero wanu woyamba ndi kuvomereza kwanu ndi zina zotero. Inu mukutenga, lenileni, thupi la Khristu.”

⁷⁴⁹ Ife timati iwo *umayimira* thupi la Khristu, mwaona, kuti si kanthu mu dziko koma chidutswa cha mkate. Ndipo ziribe kanthu ngati iwo sunali ngakhale mkate, ngati iwo ukanakhala china chirichonse, iwo ukanati udzayimire chomwecho basi. Basi—ndendende basi. Kaya iwo. . .

⁷⁵⁰ Monga anthu awa amene amanena kuti, “Ine sindingabatizidwe mu dziwe, ine ndikufuna kuti ndibatizidwe mu mtsinje.”

⁷⁵¹ Kodi izo zimapanga kusiyana kotani, bola ngati mwabatizidwa? Ngati izo ziri mu dziwe, ndi. . . Bwanji, Filipino anabatizidwa mu dziwe. . . pamene mdindoyo anabatizidwa. Pamene Filipino anamubatiza mdindo mu dziwe, Mzimu Woyera unamukwatula iye kotero kuti Iye anamutengera Filipino kutali, iye sanawoneke kwa mailosi thuu handirede. Unamugwira iye mu Mzimu, kumupatsa iye a—galeta kuchokera Kumwamba komwe kwa mailosi thuu handirede. Ameni. Zodabwitsa!

Tsopano:

Kodi oyera mtima adzakhala kuti pambuyo pa ulamuliro wa zaka-wani-sauzande? Ndipo iwo adzakhala ndi thupi lotani? Ine ndibwerera kwa ilo mu kamphindi. [M’bale Branham akuyankha funso ili pa ndime 820, monga funso 74—Mkonzi]. Iwo adzakhala ndi Yesu.

⁷⁵² Chabwino, a—funso la chiseveni:

72. Kodi tidzawaweruza motani angelo?

⁷⁵³ Izo zikupezeka mu. . . Kodi tidzawaweruza motani angelo? Pokhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Angelo ndi antchito; ife ndi ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndipo Baibulo linanena kuti ife tidzawaweruza angelo. Uko nkulondola. Tsopano, tsopano ngati inu. . .

Funso lachi 8:

73. Chifukwa chiyani tsitsi chifukwa cha angelo a Akorinto Woyamba?

⁷⁵⁴ Tsopano winawake andipezere ine Akorinto Woyamba, a—mutu wa 11, ndipo tiwona pamenepo, kuti inu mupeza kuti a—a. . . Mu Akorinto Woyamba, wa—wa 11, ife tikupeza kuti Paulo akuyankhula. Ndiroleni ine ndifike kwa izo miniti yokha, ndipo kenako ife tiwerenga izo mwamsanga ndipo kenako ife ti—tikhala nazo.

⁷⁵⁵ Ine ndiri ndi chinachake choti ndinene pa ndime ina iyi apa, chimene ine ndikuyembekeza kuti Ambuye apereka icho kwa ife momwe ife tikuyenera kukhalira ndi icho. Ngati winawake angapeze izo. . . Ine ndikuganiza uwo ndi mutu wa 11, eya, chabwino. Tsopano mvetserani mwacheru, mwacheru kwenikweni tsopano, kuchitira kuti inu mumvetse. Tsopano mutenge chikumbtima chanu chonse ndipo muchiyike icho mu thumba lanu la chovala mpaka ine nditawerenga izi, inu mwaona, kupanga ndemanga pa Izo. Mvetserani mwacheru kwenikweni, izi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE:

Khalani inu onditsatira ine, monga ngakhale ine. . . ndi wa Khristu. (Paulo anati, “Inu muzinditsata ine, monga ine ndikutsatira Khristu.”)

Tsopano ine ndikukuyamikani inu, abale, kuti inu mumandikumbukira ine mu zinthu zonse, ndi kusunga malangizo, monga ine ndinawapereka. . . kwa inu.

Koma ndingafune inu kuti mudziwe, kuti mutu wa mwamuna aliyense ndi Khristu; ndipo mutu wa mkazi ndi mwamuna; ndipo mutu wa Khristu ndi Mulungu.

⁷⁵⁶ Mukuona momwe izo ziliri? Mulungu, Khristu, mwamuna, mkazi. Tsopano:

Mwamuna aliyense akupemphera kapena akunenera, mutu wake uli wophimbidwa, amanyozetsa Khristu.

Koma mkazi aliyense akupemphera, kapena akunenera ndi mutu wake wosaphimbidwa, anyozetsa mutu wake: . . .

⁷⁵⁷ Tsopano titenga miniti yokha, ndi kukuwonetsani inu kuti tsitsi la mkazi ndi chophimba chake:

. . . pakuti izo. . . ngakhale zonse ziri ngati kuti iye anali wometa. (Izo zikutanthauza kuti ngati—ngati iye ati adule tsitsi lake, ndiye alimete ilo.)

Pakuti ngati mkazi saphimbidwa, muloleni iyenso asengedwe: (kusengedwa kumatanthauza kumetedwa, mwaona). . . *koma ngati chiri chamanyazi kwa mkazi kuti asengedwe kapena kumetedwa, muloleni iye aphimbidwe.*

758 Tsopano ife tikufika ku funso apa limene inu mukufunsa. Mukuona? Chabwino, tsopano ndi zolakwika kwa a—dona kuti amete tsitsi lake, malingana ndi Baibulo. Tsopano mvetserani pomwe pano ndipo muwone ngati Baibulo silimamupatsa mwamuna ufulu mwalamulo kuti amusiye mkazi wake ngati iye adula tsitsi lake, muwone ngati izi ziri zolondola kapena ayi.

Ngati *mwamuna . . . Pakuti mwamuna ndithudi sayenera kuphimba mutu wake* (ndiko, kukhala ndi tsitsi lalitali), pakuti mochuluka *iyeye ali mu chifanizo ndi mu ulemelero wa Mulungu: koma mkazi ali mu ulemelero wa mwamuna*. (Kodi inu munayamba mwaganizapo za izo?)

759 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiyimire apa, chifukwa ine ndikufuna kuti izi zilowerere mkati mwabwino kwenikweni, mwaona. Ndipo tsopano kumbukirani, ine ndawona makumi a masauzande a akazi okondeka (ndikuwadziwa iwo pakali pano, ndipo ochuluka a iwo akhala mu tchalitchi muno) amene ali ndi tsitsi lalifupi, amene ali Akhristu. Ndipo zomwe ndikuyikapo si inuyo, ndi momwe inu munaphunzitsidwira. Mukuona? Ndi zimenezo. Mlaliki wanu sanakuuzeni inu izi. Koma ngati aliyense wa akazi ozungulira pa kachisi ali monga choncho, ndiye iwo ndi olakwa. Mwaona, chifukwa ife ndithudi timawauza iwo za izo.

760 Tsopano, tsopano penyani izi:

. . .mwamuna . . . Pakuti . . . (ndime 7) *. . . Pakuti mwamuna . . .*

761 Tsopano, ndani akuyankhula apa? Tsopano, nthawiyina dona anati, “Oh, Paulo anali wodana ndi akazi wakale.”

762 Chabwino, tsopano pamene ife tiri pa izo, tiyeni tingotembenezira apa ku Agalatiya 1:8, ndipo tiwone zimene Paulo akunena za izi, mwaona, mu Agalatiya 1:8. Inu mupeza kuti Paulo ananena apa mu Agalatiya 1:8:

. . .ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, alalikira uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu umene inu munaumva kale, mulole iye akhale wotembereredwa.

763 Tsopano musandiimbe ine mlandu, inu mumuimbe mlandu Iyeyo, mwaona.

Pakuti mwamuna ndithudi sayenera kuphimba mutu wake, pakuti mochuluka momwe iye ali mu ulemelero ndi chifanizo cha Mulungu: koma mkazi ali mu ulemelero ndi chifanizo cha mwamuna.

764 Tsopano penyani ndime yotsatira:

Pakuti mwamuna si wa mkazi; koma mkazi ndi wa mwamuna.

Ngakhalenso mwamuna sanalengedwere mkazi; koma mkazi analengedwera mwamuna.

⁷⁶⁵ Tsopano, ine ndikutanthauza izi tsopano ndi chikondi chenicheni ndi kukoma, ndipo ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa izo momwe ine ndikunenera izi. Koma Amerika . . . Monga woyenda wapadziko lonse lapansi, Amerika ali ndi otsikitsitsa kwambiri, malamulo otsika kwa akazi awo a mtundu uliwonse padziko lapansi. Paris, France akhoza kukhala nyumba yayitali mmbali mwa momwe Amerika amalolera kuti akazi ake azichitira. Ndi zamanyazi!

⁷⁶⁶ Kodi inu munazindikira kuti mulungu wa America ndi mkazi? Ine ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu mwa Baibulo ili. Uko nkulondola. Kodi inu mukuzindikira kuti izo zikuyenera kubwera mwanjira imeneyo kuti mpingo wa Katolika ukhoze kubweretsamo chiphunzitso chawo cha namwali Mariya?

⁷⁶⁷ Tsopano, ngati mkazi sanapangidwe chifukwa cha mwamuna, osati. . . Ngati mwamuna sanapangidwe chifukwa cha mkazi, koma mkazi anapangidwira mwamuna, ndiye inu mungamupembedze bwanji mkazi? Mukuona? Tsopano, chinachita izo ndi chiyani, izo zinayambira ku Paris ndipo zinakafika ku Hollywood. Tsopano Paris ikuyenera kubwera ku Hollywood kuti idzatenge zitsanzo zawo ndi kudzatenga mafashoni awo ndi zinthu, ndi kunyozetsa kwa akazi athu aku Amerika.

⁷⁶⁸ Ndi chiyani chimenecho? Fuko lathu lachepa kwambiri mpaka kuti iwo amulanda ntchito mwamuna, ndipo akawayika akazi kunja kuno mu malo awa, mpaka nainte peresenti a iwo, pafupifupi, ndi achiwerewere. Ndipo kunena za amuna kuti apita, ndithudi, ndi chifukwa chakuti iwo ali ndi akazi kunja uko mu ntchito zawo. Ndipo iwo afika potsika-pansi kwambiri mpaka awayika akazi ngati osungitsa mtendere pa msewu. Chimenecho ndi chamanyazi kwa fuko lililonse! Inde, bwana. Kodi muchita nazo chiyani izo?

⁷⁶⁹ “Kodi inu mukuchita nazo chiyani izo, M’bale Branham?” Ine ndikuyenera kuzilemekeza izo, ndine nzika ya Amerika, ndimachita chimene bwana wamkulu akuti ndichite. Ngati ine konse. . . Ngati a—ngati banja litaya ulemu wake kwa banjalo (ana kutaya ulemu kwa kholo), banja limenelo lang’ambika mzidutswa. Ngati a—ngati mpingo utaya ulemu kwa abusa ake, bwanji, mpingo umenewo wapita. Ndipo ngati fuko litaya konse ulemu wake wa Khoti Lalikulu ndi lingaliro lake, fuko limenelo lapita mu zidutswa. Ndiko kulondola ndendende. Ife tikuyenera kulemekeza zinthu zimenezo chifukwa iwo ndi abwana aakulu, mwaona. Koma uko sikulondola kuyamba nkuyamba. Mwamtheradi!

⁷⁷⁰ Kodi inu mumadziwa kuti mwamuna mu Baibulo. . . ya Genesis, mutu wa 1, pamene Mulungu analenga mkazi ndi—

ndi mwamuna, ndipo anamupanga mwamuna ndi akazi, ndipo Mulungu anamuza Eva kuti “Mwamuna wako adzakulamulira iwe, adzakhala wokulamulira wako”? Uyankhule zimenezo mu Amerika ndipo uwone kumene ungapite! Mnyamata, si zimenezo, mkazi akulamulira pa mwamuna; iwo akuyenera kuchita zimenezo, malo a aliynse akhazikitsidwa . . .

⁷⁷¹ Ine ndikhoza kuwaberetsa akazi, ngati ine ndikanati nditero, kuchokera ku chipinda changa uko, mwa madazeni, a akazi abwino . . . ine sindikunena kuti akazi onse sakuyenera kugwira ntchito nthawizina; mwinamwake iwo ali ndi mwamuna wodwala kapena chinachake, ndipo iwo akuyenera kuti azigwira ntchito. Koma ngati iwo sakuyenera kuteru, iwo sakuyenera kuchita zimenezo. Malo awo ndi kunyumba, kanyumba kawo kakang’ono, ndi kumene iwo akuyenera kumakhala.

⁷⁷² Ndipo akazi athu Achimerika akhala ndi mwayi wopita ndi kukadya nkhumba kapena kufa. Ngakhale mwa nyama zonse ndi zina zotero, pamene chinthu chimenecho chipambana, icho chimachitika ndipo icho chimanyozetsa mtundu wonse wa icho.

⁷⁷³ Kuli mbalame yaying’ono ku Afrika, ndipo iyo ndi mbalame yaing’ono yotola.

⁷⁷⁴ Tsopano, kawirikawiri, yaikazi nthawizonse imakhala yonyansa kwambiri pa ziwirizo. Yamphongo nthawizonse imakhala yokongola kwambiri, gwape wamphongo, mbawala yamphongo, nkhangamphongo, a—nkukhu yayimuna, ndipo nthawizonse ndi mochuluka . . . Chifukwa, yaikazi ndi mbalame yakunyumba. Iyo imakhala pa chisa, iyo imalera ana ake. Iyo imadzibisa kwa nkhwangwala, njokayo, nkhandwe, china chirichonse, mwaona, kuti alere ana ake aang’ono.

⁷⁷⁵ Koma mu mpikisano kumene a . . . kapena mu gulu limene—limene—limene mkazi, kapena chachikazi, zimapambana mu kukongola, nthawizonse zimakhala zonyozeka. Mu Afrika, ukatenga mbalame . . . Kuli mbalame yaying’ono kumeneko, ndipo imodzi yokhayo pa mayiko imene ine ndikuidziwa, kuti yayikazi ndi yokongola kwambiri kuposa yaimuna. Ndipo pamene izo zotero . . . Imeneyo—mbalame imeneyo ndi yachiwerewere mowirikiza. Iyo imathamanga ndi kukapeza bwenzi, ndi kuthamangira kunjani ndi kukayikira mulu wa mazira iyo itakomana ndi imodzi, ndi kusiya bwenzi kukhalira mazirawo pamene iyo ikupita kukasaka wina. Ndiko kulondola ndendende. Mukuona? Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁷⁷⁶ Mu, tsopano penyani, mu Amerika lero, za akazi athu. Mnyamata waku Kentucky anandiiza ine, masiku angapo apitawo, kuti panali akazi eyiti handirede ogwira ntchito pa fakitale ina kuno mu Kentucky. Ndipo anati, “Ine mwinamwake ndikhoza kumverera kutetezeka nditalumbira kuti foro handirede a iwo ndi mwamtheradi mahule a mumsewu, ndipo

akazi okwatiwa ali ndi ana.” Mnyamata wina anakamuchotsa mkazi wake kumeneko ndipo anamumenya iye ndi bolodi, ndiyeno iye anakhala ngati amuphe iye. Ndipo wina anapita kukamuwombera mwamuna. Ndipo wina kuchekana ndi kumenyana. Izo zisamatero. Izo si zolondola.

⁷⁷⁷ Kamuikeni mkazi ku kitchini kumene ayenera kumakhalako, ndiye chirichonse chidzakhala bwino. Koma mukakamuika iye kunja uko pa ntchito zapagulu, iye wapita. Mwamthe- . . . Ine sindikunena kuti . . .

⁷⁷⁸ Azimayi aku Amerika amakweza mphuno zawo ndi kuti, “Palibe kanthu kwa Izo.” Ndi, “Inu mundiwonetse ine.” Ndithudi, inu mukuyenera kuti muchite zimenezo, chifukwa Baibulo linaneneratu kuti inu mudzachita izo. Inu mukuyenera kuchita izo.

⁷⁷⁹ Ndipo apa pamene . . . Izo zinalipo, kalekale, mu mpingo wa Methodist, ngati mkazi adula tsitsi lake, iye ankachotsedwa mu mpingo. Ndithudi, iwo ankachita zimenezo. Inde, ndithudi. Anazarene, a Pilgrim Holiness, Achipentekoste, onse a iwo ankachita zimenezo. Chinachitika ndi chiyani?

⁷⁸⁰ Inu mukudziwa chifukwa chake? Inu muli ndi ena achikazi kuseri kwa guwa. Ndiko kulondola ndendende. Winawake akuwopa tikiti yake ya chakudya . . . akuwopa kuti inu mungawachotse iwo, kuwathamangitsa iwo mu mpingo. Iwo analibe nkomwe kulimba mtima kuti ayime, kuyima pa Mawu a Mulungu kaya Iwo apweteka kapena Iwo satero. Ndiko kulondola ndendende.

⁷⁸¹ Mvetserani apa, mwamuna ndi wolamulira. Musaganize kuti inu mudzalamulira mnyumbamo. Inu sindinu wolamulira wa mnyumbamo. Ndinu mwamtheradi . . . Sindinu kapolo tsopano, koma ndinu wothandizira. Ndipo Adamu . . . Mwamuna ali ndi ulamuliro pa mkazi wake, ndipo iye ali ndi udindo kwa mkazi wake yekha. Mulungu amapangitsa mwamuna kukayankhira mkazi wake. Tsopano, werengani ndipo muwone ngati Mulungu akunena zimenezo tsopano.

Pakuti mwamuna ndithudi sakuyenera kuphimba mutu wake, mochuluka momwe iye ali mu chifanizo ndi ulemelero wa Mulungu: . . .

⁷⁸² Mulungu si mkazi, Mulungu ndi Mwamuna. Inu mukudziwa pamene iwo amamupanga namwali Mariya ndi zonsezo, ndi kupembe- . . . kapena kupembedzera ndi chirichonse monga choncho, ndi kupemphera kwa namwali Mariya, inu mukudziwa chimene icho chimandikumbutsa ine? Mulungu wamkazi wamkulu Diana, amene Paulo anamudzudzula ndi kumupondereza. Uko nkulondola. Iye anati, “Bwanji, Mulungu si mkazi!”

⁷⁸³ Mwala unagwa m’ munda, ndipo iwo anati mulungu wamkazi anaponya pansu fano lake, ndi chifukwa chake mkazi ku

Korinto, ndi kumtunda uko, a . . . amene ankapembedza Diana, iwo ankafuna kuti akhale alaliki.

⁷⁸⁴ Iwo anati, “Bwanji, mzimu unatiuza ife kuti tikhoza kumalalikira.”

⁷⁸⁵ Iye anati, “Chiyani? Kodi Mawu a Mulungu anatuluka mwa inu, ndipo iwo anachokera kwa inu nokha? Ngati munthu aliyense ayesa kuti ndi wauzimu kapena mneneri, muloleni iye avomereze chimene ine ndanena ndi malamulo a Ambuye: mulole mkazi akhale chete ndipo akhale womvera mu mpingo, osati kuphunzitsa, kapena kukhala ndi ulamuliro uliwonse.” Ndizo ndendende! Ndicho chimene Lemba linanena. Mukuona? Ndipo Mulungu adzapangitsa gulu la alaliki kuyankhira pa izo pa Tsiku la Chiweruzo.

⁷⁸⁶ Chabwino, mvetserani! Inu mukuti, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu, ine ndinaphunzitsidwa zimenezo.” Inu mukudziwa bwino tsopano! Uko nkulondola. Ngati inu kapena winawake ayamba kumwa mankhwala, ndipo wina nkukuuzani inu kuti ndi arsenic, ndipo inu—ndipo inu nkumapitirira nazo ndi kuwatengabe iwo mulimonse, limenelo likhala vuto lanu zikadutsa pamenepo. Mukuona?

⁷⁸⁷ Tsopano mvetserani kwa izi:

Pakuti mwamuna si wa mkazi; koma mkazi ndi wa mwamuna.

Pachifukwa ichi mkazi akuyenera kukhala ndi mphamvu pamutu pake chifukwa cha angelo.

⁷⁸⁸ Aliyense wa inu mukuwerenga izo? Akorinto Woyamba, mutu wa 11, ndi ndime ya 10. Ngati mungazindikire, “mphamvu,” (Chifukwa?) “za angelo,” Akorinto Woyamba, chifukwa angelo ndi munthu, mthenga. Taonani, ndi “a” wamng’ono kachiwiri. Kumene Angelo akukhudzidwa, za Angelo Akumwamba, ndi wamkulu “A,” chilemba chachikulu “A.” Pamene pali chilemba chaching’ono “a,” ndi anthu angelo.

Komabe palibe mwamuna . . . kapena mkazi, . . . ngakhalenso mkazi sakhala wopanda mwamuna—mwamuna, mwa Ambuye.

Pakuti monga mkazi ali wa mwamuna, choteronso mwamuna nayenso ali wa mkazi; . . . zinthu zonse ndi za Mulungu.

Dziweruzeni . . . nokha: kodi ndikoyenera kwa mkazi kupemphera kwa Mulungu (ali ndi tsitsi lalifupi) wosaphimbidwa? (taganizani za zimenezo tsopano)

⁷⁸⁹ Tsopano penyani:

Kodi chirengedwe chomwe sichimakuphunzitsani inu, kuti, ngati mwamuna ali ndi tsitsi lalitali, . . .

790 Kunena, “Kodi izo zinkakhudza chiyani?” Tsitsi. Kodi inu simukuwona chimene Paulo akunena? Tsitsi, tsitsi lalitali! Ngati. . . Mkazi akuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali. Ndime ya 14 tsopano:

Kodi chirengedwe chomwe sichimakuphunzitsani inu, kuti, ngati mwamuna akhala ndi tsitsi lalitali, ndi chamanyazi kwa iye?

791 Inu mukumvetsa zimenezo? Ndi chamanyazi kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali, koma mka- . . . amenewo ndi malo a mkazi. Mulungu anamupanga mwamuna mosiyana ndi mkazi, ziwalo ndi mawonekedwe, ndi mu china chirichonse. Iye sayenera kuvala chovala. . . Baibulo linanena kuti “Ngati mkazi avala thalauza kapena chovala chirichonse choyenera mwamuna, ndi themberero ndi chodetsedwa ndi chonyansa pamaso pa Mulungu.” Ndipo Mulungu adzapangitsa iye kulipira chifukwa cha izo. Kodi inu mumumvera ndani? Koma ili ndi Baibulo!

792 Ndipo inu mumathamanga ndi kukati, “Bwanji, ine ndikuganiza kuti izo ndi zabwino kwa. . . kuwona akazi atavala zazifupi.” Koma Mulungu anawapanga iwo mosiyana, Iye amafuna kuti iwo azivala mosiyana.

793 Ndipo Baibulo linati, “Ngati mkazi avala ngakhale chovala choyenera mwamuna, ndi chonyansa.” Inu mukudziwa chimene *chonyansa* chiri? Ndi “chinachake chimene chiri chonyansa pamaso pa Mulungu.” Ndipo Yehova Wamkulu Amene amayang’ana pansu pa inu monga ngati chinthu chonyansa. . . Ndipo Baibulo linati. . .

794 Ndipo inu amene mumati. . . Ena a inu madona tsopano, kwa atsikana anu aang’ono a zaka zammadini, eyitini, usinkhu wa zaka twente zakubadwa, kuwalola iwo azithamanga kunjaku kuno atavala monga iye aliri!

795 Ndipo inu, nanunso, amayi! Mukuona? Pamene inu mutuluka ndi kumakavala zazifupi zimenezo ndi zinthu ndi kumakhala. . . ndi kumapita pa msewu, ndi—ndi kumakakhala ndi zovala zakale izo zimene iwo akupanga masiku ano, ndi kumakupangani inu kumawoneka ngati chinachake chimene inu simuli. Mukuona? Ndipo inu mumapita kunjaku uko pa msewu mukuwoneka mwa kugonana, inu mukhoza kukhala wosalakwa ndi woyera pamaso pa mwamuna wanu ndi chirichonse, koma ngati mupita pa msewu ndipo mwamuna nkuyang’ana pa inu chifukwa inu munadziwonetsera nokha monga choncho, ndinu wolakwa, ndipo mudzakayankha pa Tsiku la Chiweruzo chifukwa chochita chigololo ndi mwamuna aliyense amene ankayang’ana pa inu monga choncho. Ndicho chimene Baibulo linanena.

⁷⁹⁶ Baibulo linati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi kuti amusirire iye, wachita naye kale chigololo mumtima mwake,” ndipo ndinu olakwa ndipo mudza . . .

⁷⁹⁷ Inu mudzafika pa Chiweruzo ndikuti, “Ambuye, Inu mukudziwa mtima wanga; ine sindinachitepo chigololo, ndinkakhala moona kwa mwamuna wanga.”

⁷⁹⁸ Koma apa padzakhala mwamuna, apa padzakhala wina, apa wina, wina, wina, wina, fifitini, twente, sarte, forte a iwo atayima pamenepo akuti, “Mulandu wa chigololo!” Bwanji? Mwamuna wina anayang’ana pa inu.

⁷⁹⁹ “Chabwino, ine ndinalibe chochita ndi izo.” Chabwino, chifukwa chiyani inu munadziwonetsera nokha monga choncho? Pamene Mulungu anakuwuzani inu kuti musamavale zimenezo, zinali zonyansa kuchita izo, ndipo inu mumapita kukamvetsera kwa *Ndani Amamukonda Susie*, kapena ndi chiyani chimenecho . . .

⁸⁰⁰ Kodi munafufuza zomwe zinachitika ndi mwamuna wa *Ndani Amamukonda Susie*? Inu nonse munaziwona izo apa posachedwapa mu pepala. Pamene ife tinali uko ku Casper, Wyoming, izo zinatulukira. Ndipo dzina lake ndi ndani? Mnyamata uja amene . . . pa *Ife Timamukonda Susie* ameneyo, kapena ndi chiyani mu—icho chinali chiyani mdziko? A . . . Oh, chimene inu nonse mumakhalira kunyumba Lachitatu usiku ndi kuphonya msonkhano wa mapemphero kuti mukawone. Ndi chiyani chimenecho tsopano? *Ife Timakonda* . . . Dzina lake ndi chiyani? [Mlongo akuti, “*Ine Ndimamukonda Lucy*.”—Mkonzi]. *Ine Ndimamukonda Lucy*, mwamuna wake, yemwe amayenera kukhala, amamenya mozungulira, wagwidwa uko ku Reno, Nevada, ndi mtsikana wachikuda, wakhala akukhala ndi iye kwa zaka. Ndipo icho ndi chimene inu mumakhalira kunyumba kuti muwonere mmalo mopita, kukamva Uthenga. Mayiyo anavomereza izo. Oh, chifundo! Palibe chirichonse choyera kunja kwa Yesu Khristu!

⁸⁰¹ Adalitse mtima wako, m’bale, ine—ine ndikuuza iwe—iwe mnyamata, ena a . . . Iwe ukuti, “Oh, mai, tayang’anani pa kalasilo.” Ena a—akhungubwe oyipitsitsa amene ife tiri nawo, miimba, ndi mbalame zokongola. Inu simungaziweruze mbalame ndi nthenga zake, mwaona. Chotero mungokumbukira zimenezo. Oh, mai!

⁸⁰² Tsopano penyani:

Kodi *ngakhale chirengedwe* . . . (imeneyo ndi ndime ya 14) . . . *sichimakuphunzitsani inu, kuti*, ndi chamanyazi kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali? (Izo ndi za mkazi.)

Koma ngati mkazi ali ndi *tsitsi lalitali*, ndi ulemelero kwa iye: . . .

⁸⁰³ Tsopano iye akuyankhula za chiyani? Chipewa chimene inu Achikatolika mumavala ku tchalitchi? Ayi ndithu! Chophimba pang’ono pamwamba pa mutu wanu, ndi mpango? Iye akulankhula za tsitsi lanu!

⁸⁰⁴ Tsopano! Ndipo ngati mkazi adula tsitsi lake, iye amadula ulemelero wake, ndipo saloledwa ku guwa kuti akapemphere. Mwaona, basi zomwe ananena apa, “Kodi ndi chinthu chozolowereka kwa mkazi kupita kukapemphera osaphimba mutu?” Akunena apa, akuti, “Chabwino, iye akuyenera kuti azimeta tsitsi lake.” Chotero muloleni iye ametedwe mpala ndiye. “Ndipo ngati iye atametedwe mpala,” anati, “icho ndi chopanda ulemu, ndi chamanyazi kuti mkazi achite izo.” Kenako anati, “Iye akuyenera kuphimbidwa.” Tsopano, ine basi—ine ndikungowerenga kalata ya Paulo. Inu nonse, izo ziri ndi inu, mwaona.

Koma ngati mkazi ali ndi tsitsi lalitali, ndi ulemelero kwa iye: pakuti tsitsi lake linaperekedwa kwa iye ngati chophimba.

⁸⁰⁵ Kodi ilo linati iye adzapatsidwa chipewa? Inu anthu Achikatolika kapena inu Achiprotestanti, mmodzi aliyense, amene amapita ku tchalitchi ndipo amafuna kuvala chipewa, kunena, “Chabwino, ine ndikupita ku tchalitchi, ndikuyenera kuvala chipewa.” Ayi, inu mukuyenera kulilola tsitsi lanu likule. Ndiko kusiyana kwake. Mukuona?

...pakuti tsitsi lake linaperekedwa kwa iye ngati chophimba. (Ndipo ndi chamanyazi kwa iye kubwera mu tchalitchi opanda chophimba, kupita ku guwa kuti akapemphere.)

Koma ngati mwamuna awoneka kuti ndi—kuti ndi... (Sindikuhulupirira kuti nditha kutchula mawu amenewo, c-o-n-t-e-...)... Wamakani—wamakani (inu mukudziwa chimene makani ali), ife tiribe mwambo wotero, ngakhalenso Mpingo wa Mulungu.

⁸⁰⁶ Tsopano ngati inu mukufuna kutsutsa za izo, inu muzitsutsana Izo. Chabwino, ngati mukufuna kukhala wamakani za izo, “Oh, izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Tiyeni tiwalole iwo apite patsogolo. Bwanji, ine ndikuganiza kuti izo si kanthu. Ine... Si chimene tsitsi liri, mulimonse, ndi chimene mtima uli.” Izo ndi zoon; ngati mtima uli wolondola, tsitsi likhala lolondola (Uh-huh).

⁸⁰⁷ Pitirizani, ngati inu mukufuna kukhala amakani, Paulo anati, “Ife tiribe mwambo wotero, ngakhalenso Mpingo wa Mulungu.” Anati, “Ngati inu mukufuna kukhala wa mbali ya Kaini, chabwino, pitirirani nazo.” Koma Izi ndi zimene Paulo ankanena.

⁸⁰⁸ Oh, ndipo ine sindikutanthauza kuti ndiseke, chifukwa si nkhani yoseketsa. Koma ndikukuuzani inu abwenzi, ndi

zochititsa manyazi kuwona mmene zinthu izi zaloledwa kuchitidwa. Ine . . .

⁸⁰⁹ Mvetserani! Kwa inu, alongo anga okonedwa, ine ndikufuna inu kuti muziwoneka mopambana kwambiri ndi kukhala mopambana kwambiri, ndi chimene inu mukuyenera kukhala. Icho ndi chimene inu mukuyenera kukhala. Ndipo inu mukuyenera kukhala okoma ndi atsopano ndi chirichonse momwe inu mungathere pamene mwamuna wanu abwera, mofanana basi monga uyo anali wokonedwa wanu. Ndipo inu mukuyenera kukomana ndi iye pakhomo ndi basi—ndi kupsyopyona basi mokoma kwa iye monga mmene zinaliri tsiku limene munamupsyopyona iye pa guwa kuti akhale mwamuna wanu. Uko nkulondola. Ine sindikuyimbani mlandu chifukwa chowoneka bwino komanso kukhala wabwino kwambiri. Ndipo ine ndikufuna inu mukhale mwanjira imeneyo, Mulungu akudziwa kuti ine ndikutero.

⁸¹⁰ Kuno nthawi ina kalelo, ine ndinkayankhula ndi Jack Shuler. Ndani anamvapo za Jack Shuler? Mlaliki wotchuka kwambiri amene a Methodist ali naye. Iye anati, “Mzimayi anabwera ndipo anati . . . tsitsi lonse lakuda, ndipo akutafuna chingamu, ndi zovala zake mwatheka pa iye, anati, ‘Inu mukudziwa, mwamuna wanga sangandilekererense ine.’”

⁸¹¹ Iye anati, “Ine sindikumuyimba iye mlandu.”

⁸¹² Uko nkulondola. Tsopano, koma chimene inu mukuyenera kuchita, inu mukuyenera kukhala mu njira yoyenera. Musatenge utsopano wanu ndi kukongola kuchokera ku Hollywood, zichtsensi izo mu Baibulo, pamaso pa Mulungu. Mukhale dona, muzichita monga dona, muzivala monga dona, muzikhala a ukhondo. Muzichita monga dona, musamavale zimenezo . . .

⁸¹³ Mwamuna aliyense amene amalola mkazi wake kutuluka ndi kuvala zinthu zazing’ono izo pamaso pa amuna, ndi zinthu zazing’ono zakale izo . . . kutuluka panja pa kapinga ndi kukatchetcha pabwalo, ndi zinthu monga izo, bambo, ine ndikukuuzani inu, m’bale! Ine sindi—ine sindikutanthauza kukhala wankhanza, ine . . . Mulungu akudziwa kuti umenewo ndi mtima wanga. Koma ine ndikuyenera kutero . . . Ine ndiyenera kusintha zambiri ndisanamulole wanga kuti azichita zimenezo. Ine ndidzakhala bwana pamwamba pa phiri apo nthawizonse momwe ndingathere, inu mwaona; ndipo pamene sindingathe, ine ndidzachoka pamenepo. Uko nkulondola.

⁸¹⁴ Oh, m’bale, ndicho chamanyazi ndi chonyozetsa kuti akazi azichita zimenezo. Ndipo ine—ine sindikutanthauza, mlongo . . . Ine—ine sindikukunyozeni inu, ndikungoyesera kuti ndinene . . . Mpingo wathu kuno ulibe mamembala, anthu amangobwera kuno. Koma ino ndi nyumba ya Mulungu, ndipo ife mwamtheradi timawauza anthu kuti asamavale zinthu zimenezo. Kuti ndizo . . . inu mudzakayankha chifukwa cha

zimenezo pa Tsiku la Chiweruzo. Tsopano penyani apa. Ndipo mulole tsitsi lanu likule, mwaona, ndipo mukhale dona.

815 Tsopano:

Tsopano mu ichi chimene chiri. . . Ine ndikulengeza kwa inu sindikukutamandani inu, pakuti kuti inu mukubwera pamodzi ku. . . osati ku zabwino, koma ku zoyipa.

Pakuti poyamba pa zonse, pamene inu mubwera pamodzi mu mpingo, ine ndikumva kuti pali kugawanikana pakati panu; ndi zina zotero, . . . (izo zikupitirira tsopano ku gome la mgonero)

816 Tsopano mveterani kwa Iwo. Ndi chifukwa chake kuti angelo. . .

817 Tsopano, M'bale Palmer, ine sindikukuuzani inu pa tepi iyi inu muzilalikira chinthu chomwecho kumusi uko chimene ine ndikuchita kuno. Koma inu mukudziwa bwino ndi mwabwino, ndipo inu pokhala mlaliki, inu mukudziwa izo ndi Choonadi, m'bale. Chabwino.

818 Chotero *angelo* pano ndi “amuna.” Ngati inu mungazindikire zimenezo, M'bale Palmer, izo ziri mu kalata yaing'ono, “angelo.” Ndipo Baibulo limapitirira. . . Iye akulankhula za mwamuna ndi mkazi wake, mwaona, ndicho chimene phunzirolo liri.

819 Umo ndi momwe anthu amasokonezedwa kwambiri mu Baibulo, iwo amati, “Chabwino, Mulungu amanena chinthu chimodzi *apa*, ndi china. . .” Ayi, inu—inu mumachoka pa phunziro. Khalani pa phunziro lomwelo, ndizo zonse. Iye akulankhula za mwamuna ndi mkazi.

820 Tsopano chinthu china chimene ndikufuna kugunda tisanatseke, zinditengera pafupifupi maminiti awiri:

74. Kodi oyera mtima adzakakhala kuti ukadzatha ulamuliro wa zaka wani-handirede? Ndipo kodi iwo adzakakhala ndi thupi lotani?

821 Ine ndikuganiza ilo ndi funso lokoma kwambiri, ndikungozikonda zimenezo. Tsopano tiyeni tiwone molunjika mu izo.

822 Pachiyambi, Mulungu. . .Ife tibwerera ku chiphunzitso chatu cha Chihebri kwa maminiti ochepa chabe. Mulungu anali Kasupe wamkulu uyu wa mitundu seveni. Ndi angati akudziwa zimenezo? Mukuona? Ndipo ndi angati akudziwa kuti Mulungu ali ndi Mizimu seveni? Mwamtheradi, Mizimu seveni. Ndipo munali maso seveni mwa Mwanawankhosa, ndi zina zotero, zonsezo zikubwera pamodzi tsopano. Mukuona? Tsopano, ameneyo anali Mulungu.

823 Tsopano pamene Iye (Logos) anatuluka mwa Mulungu, amene anali Mulungu akubwera kuchokera ku kasupe wamkulu

uyu kulowa mu thupi mu mawonekedwe a—a munthu; ndipo iye anapanga Logos, imene ife timayitcha fiofane.

⁸²⁴ Tsopano, ngati inu mutenga fiofane pamene inu mukuyang'ana pa izo, ameneyo ndi mwamuna. Tsopano kuti ife . . . Tsopano, apo ndi pamene ife tinali pachiyambi. Tsopano, inu simukumvetsa izo tsopano, koma inu munali kumbuyo uko pachiyambi mwanjira imeneyo. Pamene munthu anapanga . . . Pamene Mulungu anamupanga munthu mu chifaniziro Chake, Iye anamupanga iye fiofane. Ndipo Iye anangomuika iye mu thupi . . . Pamene Mulungu anamupanga munthu mu chifaniziro Chake, mu mawonekedwe Ake, iwo anali . . . Mu Genesis 2, apo panali . . . kapena Genesis 1:28, ine ndikukhulupirira iyo ili, “Panalibe munthu wolima mu nthaka,” ndipo Mulungu anali atamulenga mwamuna ndi mkazi. Uko nkulondola, “Panalibe munthu woti azilima mu nthaka.”

⁸²⁵ Kenako Mulungu anamutsitsa munthu pansi pang'ono ndi kumuyika iye mu moyo wa nyama, limenelo ndi thupi ili, chimodzimidzi monga nyama koteru kuti iye adzathe kulima mnthaka, azitha kukhudza. Fiofane imeneyo siyimakhudza, iyo siyimawona, kulawa, kununkhiza, kumva; zokhudzira izi zomwe ife tiri nazo. Chotero Mulungu anamuyika munthu pansi apo kuti—kuti azikhudza ndi kumva.

⁸²⁶ Ndipo—ndipo pamene iye ankayenda m'munda wa Edeni, poyamba ngati fiofane (monga Mzimu Woyera uli muno tsopano ukuyenda mkati muno), iwo unatsogolera moyo wa nyama. Iwo unkalumulira chirichonse, koma iwo sukanakhoza kulima mnthaka, mwaona. Chotero Mulungu anamuyika iye mu thupi kuti iye azikhoza kulima mnthaka. Anamupatsa iye mphamvu zake faivi, kuti azilima mnthaka ndi kukonza—minda ya mpesa ndi—ndi zina zotero, ndipo kenako munthuyo ankawonekabe wosungulumwa. Oh, ichi ndi chithunzi chokongola.

⁸²⁷ Taonani, pakuti pamene iye anapangidwa koyamba, iye anapangidwa anthu awiri palimodzi. Iye anapangidwa zonse ziwiri mwamuna ndi mkazi, mwamunayo anali. Baibulo linati iye anali. Mulungu anamupanga munthu ziwiri zonse mwamuna ndi mkazi, “Iye anamulenga iye.” Zindikirani tsopano, pamene munthu analekanitsidwa kwa fiofane ndi kudzayikidwa mu thupi, iye anali—iye sikuti anangokhala zonse pamenepo; gawo la umunthu wake linali likadali fiofane, chotero izo sizinkawoneka bwino.

⁸²⁸ Apo panapita yamphongo ndi yayikazi mu ng'ombe, apo panapita kavalo, ndipo apo panapita ng'ombe, ndipo apo panapita china chirichonse, ziwiriziwiri. Koma Adamu, iye . . . izo zinali . . . Mwaona, apo panali chinachake chosowekera. Chilakolako chimenecho chinasonyeza kuti panali mzake amene ankamuyembekezera iye. Inu mukumvetsa izo? Ndipo malingaliro omwewo kuti ife tikuyenera kufa kuno, kuti ife

timavutitsidwa ndi kuzunguzika, ndipo ife timalakalaka Moyo umene ulibe imfa, izo zimasonyeza kuti iwo ukutiyembekezera ife. Mukuona?

⁸²⁹ Ndipo Adamu anali wosungulumwa. Ndipo Mulungu, kuti awonetsere kuti iwo sakanakhoza kulekanitsidwa. . . Tsopano ine ndibwereranso mu chinthu chomwechi, mphindi chabe.

⁸³⁰ Taonani, Iye sanapite konse ndi kukatenga dothi ndi kumupanga Eva, koma Iye anamupanga kuchokera ku dothi lapachiyambi, Adamu. Iye anatenga nthiti ku mbali yake ndipo anamupangira iye womuthandizira, ndipo ameneyo anali Eva. Iye anapangidwira mwamuna, ndipo gawo la mwamuna. Iye anali gawo la iye pachiyambi, mu chirengedwe, mu fiofane. Iye anali gawo la iye pansi apa mu chirengedwe ichi. Iye sakanakhoza kugawidwa mu chirengedwe china, iye ankayenera kuti apangidwe mu chirengedwe chomwecho.

⁸³¹ Ndizo ndendende chifukwa chimene Khristu ndi Mulungu ankayenera kukhala Munthu yemweyo, izo sizikanakhala chirichonse chosiyana. Ngati Iye akanakhala munthu wabwino kapena mneneri, Iye sakanakhala Muomboli; Iye ankayenera kukhala Mlengi Mwiniwake. Koma Iye akadali fiofane tsopano, inu mwaona, ndi momwe Iye analiri nthawi imeneyo.

⁸³² Tsopano munthu anabwera kuno ndipo iye—iye anali wopambana; ndipo Mulungu anazikonda zimenezo, Iye anati, “Izo ndi zokongola, asiyeni iwo akhale padziko lapansi ndipo azikhala kumeneko kwanthawizonse. Ndizo zonse; kwa—kwa Muyaya, kumapitirira ndi kumapitirira ndi kumapitirira. Zisiyeni izo zikule, ndipo mbewu iliyonse ibale, ndi chirichonse monga choncho. Ndipo musiyeni munthu akhale moyo, ndi nyama zikhale moyo, ndi china chirichonse, kwanthawi za nthawi. Izo ndi zabwino.” Mukuona?

⁸³³ Ndipo kenako tchimo linadzalowa. Ndipo ine ndikufuna kuti ndipange neno ili. Mu. . . Anthu ambiri amapanga kulakwitsa kwambiri pa Lemba limodzi ili, ndipo ilo liri pa Salmo la 23. Iwo amawerenga Ilo monga chonchi, “Eya, ngakhale ndingayende mu chigwa cha *mdima* wa mthunzi wa imfa.” Tsopano, palibepo chinthu choterocho. Baibulo silimanena, kuti, “Mthunzi wakuda wa chigwa. . . chigwa chamdima cha mithunzi ya imfa.”

⁸³⁴ Limati, “Ngakhale ndingayende mu chigwa cha mthunzi wa imfa.” Tsopano, iwo usanakhale mthunzi, iwo ukuyenera kukhala ndi kuwala kuti upange mthunziwo. Mwaona, Davide pokhala mneneri ndipo pansi pa kudzodza, iye sanalakwitse, iye anangonena Choonadi: “Inde, ngakhale ine. . .” osati, kuyenda mu chigwa *chamdima*, koma, “kudutsa mu chigwa cha *mithunzi* ya imfa.”

⁸³⁵ Ndiye inu mukuyenera kukhala ndi gawo lina la kuwala kuti mupange mthunzi. Ndipo umo ndi momwe izo ziliri pano. Ndife ziwiri zonse achithupithupi komanso auzimu.

Thupi ili ndi loyenera kufa, ndipo linabweretsedwa ndi mkazi; osati mwa kalikonse koma kupyolera... Osati ndi Mulungu, ndinu opangidwa kuchokera kwa Adamu ndi Eva. Kaya wakuda, woyera, kapena chirichonse chimene inu muli, ndinu wopangidwa, mphukira yochokera kwa Adamu ndi Eva. Izo zimapangitsa thupi lanu “lobadwa mu tchimo, lowumbidwa mu kusaeruzika, linabwera ku dziko likuyankhula mabodza.” Ndinu atsoka ndi otsutsidwa pachiyambi cha moyo wanu, osati ngakhale, opanda mwayi.

⁸³⁶ Tsopano, chifukwa mzimu umene inu muli nawo umabwera kwa inu mwachibadwa, ndipo mwa chibadwa kuchokera mu kugonana, chilakolako cha amuna ndi akazi chimabala mwana wapadziko lapansi. Ndipo mudzamusiyeye mwana ameneyo yekha, ndipo osamuphunzitsa iye kalikonse koyenera, iye adzalakwitsa. Osamuphunzitsa iye chabwino kapena cholakwika, iye adzatenga cholakwika. Chifukwa ndicho chikhalidwe chake kuti azichita zimenezo.

⁸³⁷ Muwoneni mwana wamng’ono wakale, osati wopitirira kuposa *choncho*, amangokwiya kwambiri; iye basi... iye—iye amafinya manja ake, ndi kufiira pankhope, ndi kugwira mpweya wake. Ndithudi. Ndi chiyani chimenecho? Ndi chikhalidwe chake. Iye anazitenga izo kuchokera kwa bambo ake kapena amayi ake, mmodzi; iwo anali ndi kupsya mtima kokwanira kuti amenyane ndi macheke, kapena abambo ake. Ngati iwo sanatero, agogo ake aamuna kapena agogo ake aakazi ankatero. Mwaona, ndi mphukira.

⁸³⁸ Chotero izo zimapanga... Ndinu wobadwa mdziko. Inu munabwera mwa chirengedwe, ndipo umunthu wanu wonse ndi wakuda ndi wamwaye, ndi watsoka, ndi wotembereredwa ndipo ukupita ku gehena. Uko nkulondola!

⁸³⁹ Koma pamene iwe ubadwa mwatsopano, ndiye Kuwala kwa Mulungu kumawalira pansu mu moyo umenewo (aleluya) ndiye icho sichikhalanso chigwa chamdima, koma ndi chigwa chokhala ndi mthunzi mmenemo. Inu mukhoza kuphimbidwa pano ndi mnofu, ndi zinthu pa nkhope yathu, koma muli Kuwala kokwanira mmenemo. Ndipo tsiku lina Kuwala kumeneko ndi mdima zikuyenera kudzalekana! Ndipo pamene kuwala kukawala, mdima umathawa. Ndipo pamene ife tipita kukakhala ndi Khristu mu thupi limenelo, mdima ndi imfa zimachoka, ndipo ife timatulukira mu Kuwala kwangwiro. Ulemelero kwa Mulungu! Ndi zimenezotu pamenepo; palibenso matenda, palibenso mdima wosakanikirana ndi iwo.

⁸⁴⁰ Pakali pano tiri ndi zonse ziwiri matenda ndi chimwemwe, ndipo tiri ndi thanzi ndi mphamvu, ndipo tiri ndi *zolowa* ndi *zotuluka*, ndi *zokwera* ndi *zotsika*, ndi chimwemwe ndi chisoni, zina zotero. Chabwino, ndi mthunzi chabe. Ife tiri ndi kuwala kokwanira kudziwa kuti kuli Kuwala kumeneko;

ndipo ife tikadali mu thupi, mu mnofu. Koma Tsiku lina tsiku lidzabwera. Ndi pamene mngelo wa imfa adzakhale pa phazi la bedi, ndi pamene dokotala adzanena kuti zonse zatha; ndipo zachirengedwe izi zimachokera ku zauzimu, ndipo kuwala kumabwereranso ku Kuwala, ndipo mdima umabwerera ku mdima. Zikadzatero chivundi ichi chidzavala chachisavundi. Ndi pamene chivundi ichi chidzavala chisavundi. Ndi pamene chivundi ichi chidzavala chisavundi, ndipo ife tidzakhala ochokera ku cholengedwa cha nthawi kupita ku cholengedwa cha Muyaya. Inu simungatuluke pamenepo ndi mdima wathunthu, inu mukuyenera kukhala ndi kuwala mu mdima. Ndi zimenezotu pamenepo. Limenelo ndi thupi limene inu mumalilandira.

⁸⁴¹ Kodi ife timachita chiyani? Chabwino, m'bale wanga wokonedwa woyera, mlongo wanga wokonedwa woyera, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, pamene Mulungu anakulangani mu chifaniziro chake, kapena analenga—munthu mu chifaniziro Chake, ndipo anamulenga mkazi mu chifaniziro cha mwamuna ku ulemelero wa mwamuna, Iye anakupangirani inu fiofane. Chimodzimidzi basi ngati Iyemwini, pamene Iye anati “Tiyeni Ife” kwa zolengedwa zimene Iye anali atazipanga, “tiyeni Ife tipange munthu mu chifaniziro Chathu Chomwe, mu maonekedwe Athu, fiofane.” Mulungu anali asanakhale thupi apobe, Iye anali mu fiofane.

⁸⁴² Ndipo Mose anamuwona Iye. Mose analira, “Ambuye, ndiroleni ine ndikuwoneni Inu.”

⁸⁴³ Iye anati, “Pita uko ndipo ukabisale mu thanthwe, mu mphanga.” Ndipo Mose anabwerera mu mphanga; ndipo pamene Mulungu anadutsa, mphezi ndi mabingu... Ndipo pamene Mulungu anakadutsa, Iye anali atatembenuza nsana Wake monga *chonchi*.

Ndipo Mose anati, “Iwo unali nsana wa Munthu.” Aleluya!

⁸⁴⁴ Iye anali Ndani? Melkizedeki amene anatsika, Mfumu ya Chalemu, wopanda atate kapena amayi, wopanda chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo. Ndi Iyeyo! Ndipo Iye anatsika pansu. Ameneyo ndi Mmodzi amene anayankhula kwa Abrahamu; amene anamusonkhanitsira Iye thupi laling'ono la mnofu monga choncho, ndi “Psyii!” anapumira mwa ilo, analowa mwa ilo, ndipo anatsika pansu ndipo anadya mwana wa ng'ombe, anamwa mkaka wa ng'ombe, ndi kudya batala ndi mkate wa chimanga. Ndi Angelo awiriwo.

⁸⁴⁵ Ndipo pamene iwo anayenda kunjira uko, ndipo zinthu zonsezo basi, “Psyii!” anazimirira ndipo anapita.

⁸⁴⁶ Ine sindinaganizepo za izo. Kuno nthawi ina kalelo, nditanyamula chipolopolo cha mfuti, ine ndinali ndi mfuti ya .22, ndi .220 Swift. Ndipo inu abale owombera mfuti muno mukudziwa. Chipolopolo chaching'onocho, ndi chipolopolo cha

machaka forte-eyiti, basi chachitali *chomwecho*, chipolopolo chawamba cha .22. Icho chimayikidwa pafupifupi pa mphamvu ya chipinda cha .30-06. Tsopano ine . . . Fakitare imangonyamula izo mpaka pafupifupi mafiti forte-foro handirede pa mphindi. Chabwino, koma inu mukhoza kuika zokwanira . . . kuyika izo nokha, ndipo mukhoza kuyiyika mpaka mafiti faivi sauzande pa mphindi. Ndipo—ndipo apo ayi, ngati inu mumawombera . . . Ife tinkawombera, tsiku lina, pa mayadi thuu handirede, ndipo chipolopolo chinkamenya fumbi, icho chinkawuluka mfutiyo isanalire nkomwe. Umo ndi momwe icho chinaliri ndi liwilo.

⁸⁴⁷ Ndiye mudzatenge chotokosera mmano (inu mukudziwa, gawo lafulatiro pa chotokosera mmano) ndipo mudzafikire pansu mu wonga wanu ndi kudzatenga chinthu chimenecho chodzaza ndi wonga, basi pafupifupi machaka foro kapena faivi, ndi kudzaiyika iyo pamwamba apo, ndipo kenako nkuyika chipolopolo chanu mmenemo. Mudzaima apa, ndipo inu muli ndi chipolopolo mdzanja lanu mu mphindi. Ndipo kuyiwombera iyo kunja uko pa nkumba itakhala mafiti thuu handirede kuchokera kwa inu, ndipo nkumbayo sinasunthe nkomwe. Chipolopolocho chimabwerera ku chikhalidwe chake, chapachiyambi, kubwerera ku mpweya. Apa pali chipolopolo chomwe chiri chamkuwa ndi mtovu zitasakanikirana pamodzi, ndipo mphindi imodzi yokha, icho chimabwerera mpaka inu simungachipezenso icho. Icho chinabwerera mmbuyo monga izo zinali zaka mabillions handirede zapitazo, kubwerera ku mipweya. Mipweya imeneyo imayenera kupanga ndi kubwereranso kukhala mkuwa ndi kukhala mtovu, ndi zina zotero, monga choncho. Mipweya imeneyo ikuyenera kukhazikika.

⁸⁴⁸ Tsopano, ndi zimenezotu pamenepo. Umo ndi momwe ife tiriri pano, ife timachokera ku chinthu chapamwamba. Pachiyambi ife tinali mu chifanizo cha Mulungu. Chophimba ndi mdima zimatilepheretsa ife kudziwa izo tsopano. Koma Yesu anawauza ophunzira Ake kuti Iye “anali ndi iwo maziko a dziko asanakhazikitsidwe.” Mukuona? Ife tinali! Inu simungadziwe izo tsopano, koma inu munali pachiyambi. “Ndipo ngati msasa wapadziko uwu udzapasuka, ife tiri nawo wina umene ukuyembekezera kale!” Aleluya! Ndipo kenako ife tidzasunthira mu fiofane iyi, imene ife tinakhalamo poyamba, kuti tidzakhoze kumakadya ndi kugwirana chanza. Ndipo miyoyo pansu pa guwa ikulira, “Mpaka liti, Ambuye?”

⁸⁴⁹ Pali masitepe seveni amene amapita kwa Mulungu, kwa Mizimu seveni pamene—pamene Iyo ikutsika. Chabwino, pamene inu mukupita pansu pa guwa la Mulungu, iwo anali kulira, “Ambuye, mpaka liti? Kodi ife tingabwerere, kudutsa pansu apa?”

⁸⁵⁰ Mulungu anati, “Kwa kanthawi pang’ono chabe, mpaka amzanu avutike ndi chinthu chomwecho chimene inu mwavutika

nacho.” Mukuona?

⁸⁵¹ Ndipo kenako miyoyo idzabwereranso, ndipo iyo idzakhala amuna ndi akazi kachiwiri, ndi kudzakhala moyo kwanthawizonse pamene mdima wonse ndi imfa ndi matenda ndi chisoni cha mdima zidzazimirira; kulibenso mthunzi, kudzakhala kuwala kwa dzuwa mwamtheradi!

⁸⁵² Mvetserani. Ichi ndi chimene. Mulole kuti kukhale mdima momwe kukufunira kukhala; sikungakhale mdima kwambiri mpaka dzuwa litaphwanyanya mdima uliwonse. Mdima ndi kuwala sizingakhale nthawi yaitali limodzi. Pakuti a . . . Champhamvu kwambiri ndi chiyani? Ndi kuwala. Ndipo pamene kuwala kukawala, mdima umathawa. Amen. Kodi sindinu okondwa? Kodi sindinu wokondwera kuti mukudziwa? Mosakayikira, palibe mthunzi paliponse. Koma Kuwala kodala uku kumene kuli mmitima yathu pakali pano, chinachake chikuchitira umboni mobwereza: Mwana wa Mulungu, mphamvu ya Mulungu.

⁸⁵³ Ndipo ife tikuyenda muno, tikuwona mphamvu ya Mzimu Woyera ikutsika pansu ndi kumapita mu msonkhano, ndi kumati, “Inu munali Akazi a *Akuti-ndi-akuti*, kuti inu munachita chinthu *chinachake*, ku malo *enaake*. Inu mwakhala ndi mliri ndi izi nthawi yaitali *chomwechi*, koma PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Imirirani pa mapazi anu, inu mwachiritsidwa.’” Ndipo wolumala ndi wakhungu kuimirira pa mapazi awo. Ndipo mthunzi wa munthu, utadyedwa ndi khansa, kuwuka ku moyo ndi thanzi latsopano kachiwiri.

⁸⁵⁴ Palibe kukaikira, Yesu anati, “Zinthu izi zimene Ine ndikuchita, inunso muzidzazichita.” Ndipo Iye anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate andisonyeza Ine.”

⁸⁵⁵ Ndi chiyani chimenecho? Ndiko Kuwala kumene kwabwera kudzasanganikirana mu mdima uwu, inu mwaona, kudzatiwombola ife. Mukumvetsa zomwe ndikutanthauza?

⁸⁵⁶ Tsopano, tsiku lina zidzabwerera kumeneko, ndipo kenako pamene fiofane idzakhale mnofu wachisavundi kachiwiri monga izo zinali pachiyambi, ndiye Yesu adzabwera, ndipo Mulungu . . . pamene Khristu adzakhale mmodzi. Khristu adzakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anthu onse adzakhala anthu. Khristu adzakhala pa mpandowachifumu wa Davide, Munthu, Ambuye Yesu; osadzafa konse. Ife sitidzafa konse, ife sitidzadzala konse, sitidzakhala konse ndi chisoni, ndipo tidzakhala moyo kudutsa zaka sauzande.

⁸⁵⁷ Ndipo pamene zaka sauzande zidzatha pa dziko lapansi, ndiye mdierekezi adzaza; ndipo chiwukitsiro chachiwiri chidzabwera, chiwukitsiro cha osalungama. Iwo adzasonkhanitsa khamu lalikulu ngati mchenga wa kunyanja, ndipo iwo adzabwera kudzazungulira msasa wa oyera mtima,

ndipo pamene zidzatero, Mulungu adzavumbitsa moto ndi sufure kuchokera kumwamba ndi kudzawawononga iwo.

⁸⁵⁸ Ndipo Yohane anati, “Ine ndinawona kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, pakuti kumwamba koyamba ndi dziko loyamba zinachoka, ndipo kunalibenso nyanja. Ndipo ine, Yohane, ndinawona Mzinda Woyera, Yerusalemu Watsopano, akutsika kuchokera kwa Mulungu Kumwamba, wokonzeka ngati mkwatibwi wokongoletsedwera mwamuna wake.” Ndi inu pamenepo.

⁸⁵⁹ Pamenepo iye anati, “Mkazi...Mwanawankhosa ndi Mkwatibwi adzakhala kumeneko kwanthawizonse.” Padzakhala dziko latsopano, mamillioni ndi mamillioni a mailosi mbali zonse. Oh, mai. Mzinda, Baibulo limawuyeza Mzinda wa mailosi fifitini sauzande mbali zonse. Iwo ndi mailosi fifitini sauzande kutalika, mailosi fifitini sauzande kutambalala, mailosi fifitini sauzande mmwamba. Ndizo ndendende kulongosola kumene Baibulo limapereka kwa Mzindawo. Nzosadabwitsa kuti kulibenso nyanja, kunalibe malo ake.

⁸⁶⁰ Oh, kudzakhala kukongola koteroko! Ndipo mmenemo, pali kasupe pa Mpandowachifumu wa Mulungu pomwe, amene amayenderera patsogolo pa Mpandowachifumu. Pali mtengo mbali zonse za mtengowo...za mtsinje wa Moyo. Ndipo mu mtengo uwu muli mitundu thwelovu ya zipatso, ndipo umabereka zipatso zake mwezi uliwonse.

⁸⁶¹ Pali akulu twente ndi foro. Ndi ameneyo Mkwatibwi. Apo pali forte ndi foro sauzande, adindo a mkachisi. Oh m’bale, ife tikupita kwinkwake! Zinthu ziri patsogolo pathu. Foro... Akulu twente ndi foro. Adindo forte-foro sauzande. Mkwatibwi atakhala ndi Khristu. Mai, inu mukukamba... Kwathu kwa Ine, Kwathu kokoma! Amen.

⁸⁶² Kuganiza kuti ndiri ndi mwayi wopita kumeneko, ndipo inu muli ndi mwayi wopita kumeneko. Ndipo inu mungasankhe bwanji kuyenda mu mdima uwu ndipo osawona Kuwala, ndi kufa ndi kupita mu chisokonezo ndi kukhala opanda kanthu? Pakuti pamene Kuwala kutenga ulamuliro wake wapamwamba, sipamakhala malo a mdima. Pitani mukafufuze kumene mdima umapita pamene kuwala kwabwera. Izo pamene izo ziri, pamene zinthu zonse zitembenezidwira kwa Mulungu. Izo zinali, mdima unali ndi chiyambi, mdima uli ndi mathero. Kuwala kunalibe chiyambi kapena kulibe mathero. Mulungu analibe chiyambi kapena alibe mapeto. Koteru, tsiku lina, dziko lonse lotayirira ndi tchimo lake lonse ndi kukongola kwake, lotchedwa chomwecho, ndi zabwino zake zonse ndi zogirigisha, ndi kukongola kwake konse ndi chirichonse zidzazimirira nkusakhhalanso kanthu, ndipo ilo

silidzakhala ponso. Ilo silidzakhala ponso, osazaganiziridwanso! Ilo linati, ngakhale, “Ilo silidzabweranso mu chikumbutso.”

⁸⁶³ Koma odalitsika a Ambuye nthawizonse adzakhala ndi Iye. Ife tidzakhala nalo thupi ngati Thupi Lake Lomwe laulemelo; ndi kudzakhala ndi Iye, ndi kudzadya ndi Iye, ndi kudzakhala ndi Iye, ndi kukhala ndi Iye kwanthawi za nthawi ndi manusu a nthawi; ndipo mibadwo Yamuyaya idzapitirira ndi dziko lopanda mathero.

⁸⁶⁴ Ndipo inu muli ndi chisankho usikuuno. Ngati simunakonzekere kukumana ndi malo amenewo, ziribe kanthu kuti mumapita ku tchalitchi mochuluka bwanji, ndinu membala wabwino chotani, inu ndi wotaika mpaka Khristu atakupatsani inu Moyo watsopano mu mdima uwo umene inu mukuyendamo. Inu mukhoza kukhala achipembedzo. Achipembedzo, mveterani, abwenzi, chipembedzo ndi luntha. Mukuona? Ana onse a Kaini akhala nthawizonse ali ndi chipembedzo. Ayuda amenewo anali ndi chipembedzo pamene Yesu anabwera, koma iwo anakana chipulumutso.

⁸⁶⁵ Inu mukhoza kukhala achipembedzo kwambiri usikuuno. Inu mukhoza kukhala Presbateria, Methodisti, Pentecostal, Nazarene, Pilgrim Holiness. Inu mukhoza kungokhala wachipembedzo basi; kumapita ku tchalitchi chanu ndi kukachitira umboni, mukhoza kumaimba ndi kufuula ndi kumutamanda Ambuye, inu mukhoza kumabwera zakhumi zanu ku tchalitchi, mukhoza kuwachitira zabwino oyandikana nawo anu, zimenezoyiribe kanthu kamodzi kochita ndi kopita kwanu Kwamuyaya. Kaini anachita chirichonse cha izo. Mwamtheradi.

⁸⁶⁶ Baibulo linanena kuti “tirigu ndi namsongole zimabwera pamodzi.” Tirigu wamng’ono wokhazikika, amakhala ndi njala ya mvula, ndipo—ndipo minga nayonso. Pamene mvula ibwera, minga zimangosangalala basi kuti zalandira mvula ngati momwe tirigu angachitire. “Koma, ndi mwa zipatso zawo, inu mudzawadziwa iwo.”

Tsopano tiyeni tipemphere pamene inu mukufufuza zipatso zanu.

⁸⁶⁷ Tsopano, Atate Mulungu, pakhala pali mafunso ena olimba pano usikuuno. Ine mwinamwake sindinachite chinthu choyenera, koma kupambana kwa kudziwa kwanga; Inu mukuwudziwa mtima wanga. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwulandire iwo. Ndipo tsopano, mwinamwake, mu ena a mafunso awa, ngati ine sindinawapange iwo molondola, ndiye Inu muyankhule ku mitima ya anthu, ndipo Inu muwapange iwo kumene iwo akuyenera kukhala. Ine ndikumverera kuti Inu munandiuza ine. Koma ngati ine ndingalakwitse, ndiye Inu mundikhululukire ine.

868 Ndipo ndikupemphera, Mulungu, kuti aliyense wa awa atenge zinthu izi mu mtima mwawo, ndipo mulole iwo alingalire pa izo ndi kuganiza monga chonchi, “Inde, ulipo mpingo, ziripo zinthu izi. Ndi chimene Baibulo linanena.”

869 Mwinamwake madona, Ambuye, Inu mukudziwa ine sindinatanthauze chirichonse chandekha powauza iwo. Koma, Mulungu, ine—ine ndimawakonda alongo anga, ndipo Inu mukudziwa zimenezo, Atate. Inu mukudziwa momwe ine ndimaganizira za iwo. Koma kuti ndiyime ndi kuwauza iwo chinachake cholakwika, ine ndingakhale—wachinyengo kwa iwo. Ine sindikufuna kuti ndikhale wachinyengo kwa alongo anga, ine ndikufuna kuwauza iwo Choonadi. Ndipo, Atate, ine ndikuzitenga Izo kuchokera mu Mawu Anu omwe.

870 Ndipo tsopano ine sindikuwatsutsa abale anga, koma, Ambuye, ine ndikunena kuti iwo akhala akulakwitsa pamene iwo aloleza zinthu izi. Ndipo ngati donayo anadziwa mosiyana ndipo anapita nakachita izo, ndiye izo ziri kwa iye, abusa alibe mlandu.

871 Abba Atate, zinthu zimenezo ndi Mawu Anu, ndipo izo ziri kwa Inu. Tsopano Inu muyankhule ku mitima ya anthu. Ine ndikuwapereka iwo onse kwa Inu. Ine ndiwona chimene Inu mwachita, Atate; Inu mukudziwa. Muyankhule kwa mtima uliwonse. Ife tikupempha mu Dzina la Khristu.

Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa:

872 Ndikudabwa ngati wina angakweze dzanja lake, ndikuti, “M’bale Branham, mungondikumbukira ine kuti ine ndikhale mgonjetsi wathunthu, ndipo pa tsiku lomaliza kudzavala chovala chaukwati ndi kudzakhala ndi Khristu.” Kodi mungakweze dzanja lanu, ndikuti, “Mundipempherere ine”?

873 Aliyense ikani mutu wanu pansu tsopano, ndipo mungowerama. Mulungu akudalitseni inu, izo ziri bwino. Pamenepo, Mulungu akudalitseni inu, alongo anga; ndi abale anga, nanunso, mukukweza manja anu. Izo ndi zopambana.

874 Tsopano, Atate, Inu mukuona manja awo. (Ine ndikudziwa, nthawizina inu mumaganiza, “Chabwino, kapemphero kakang’ono chabe ngati kameneko?”) Mulungu, ndikuganiza za amayi aja, ananena dzulo, “Pemphero laling’ono chabe uko mnyumba yake tsiku lija pamene mnyamata ameneyo ankafa, masabata atatu kuti akhale moyo, chotupa chimenecho pa ubongo, ndipo tsopano kusintha zinthu.”

875 Ine ndikuganiza za Hezekiya, atatsamira nkhope yake kukhoma, ndi kumalira, “Ambuye, ine ndikukupemphani Inu, mundichitire ine chifundo. Ndiganizireni ine, pakuti ine ndayenda pamaso Panu ndi mtima wangwiro.” Izo zinasintha kuchoka ku imfa kupita ku moyo.

876 Kufuula kumodzi kuchokera kwa Mwana wa Mulungu, “Lazaro, tuluka!” ndipo munthu wakufa anatuluka.

877 O Mulungu, Inu munati, “Lankhulani, pemphani, ndipo zidzaperekedwa. Pamene munena chirichonse, mukhulupirire kuti chimene inu mukunena chichitika, inu mudzakhala ndi chimene mwanenacho.”

878 Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti aliyense amene anakweza dzanja lake alandire chimene iwo anakwezera manja awo. Ndipo mulole iwo adalitsidwe. Ndipo Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muwathandize alongo athu, kuti iwo akhale...mulole iwo adzikhaliitse okha akhalidwe, kuti Satana kupyolera mu televizioni ndi magazini a *True Story* ndi zina zotero, zimene zakhala zikugwiritsidwa ntchito momasuka kwambiri, ndi maprogramu osasefedwa, momwe zodetsedwa ndi zonyansa pa televizioni ndi zina zotero, zomwe zikanati...Zikanakhala chida chopezera mamillioni a miyoyo kwa Inu, koma momwe izo sizikusefedwa, ndi kuchotsa zinthu zonse zauve zakale zimene iwo...Oh, ndi zachisoni bwanji! Ndipo kudziwa kuti mzimu wa mdierekezi walowa mkati ndi pozungulira alongo athu, ndipo akuyesetsa kuwapangira iwo mafashoni ndi kuvala monga choncho.

879 Ndipo ife tikupeza kuti mu...mwa abale athu, nawonso, Ambuye, momwe iwo amadziwira kuti akhoza kusuta ndi kumwa, ndi kumapitirira monga choncho, ndipo nkukhalabe Akhristu chifukwa iwo amati iwo “amakhulupirira.” Mulole iwo adziwe kuti “mdierekezi amakhulupirira, nayenso.” Ndipo iye sanapulumsidwe, “iye amakhulupirira ndipo amanjenjemera.”

880 Ndipo tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mukhale achifundo kwa ife tonse, ndipo mutikhululukire ife machimo athu, ndipo mwinamwake ena sanakweze manja awo mmwamba, O Mulungu, achitireni chifundo. Mulole mwayi wotsatira umene iwo adzakhale nawo, mulole iwo adzakweze manja awo.

881 Ife tikukonzekera kutenga mgonero, Ambuye. Tikhulukireni ife zolakwa zathu ndi zakale zathu za moyo. Ndipo mulole ife tilandire mdalitso Wanu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amen.

882 Ambuye akudalitseni inu. Pepani kuti ndakusungani inu monga chonchi. Ine ndikungodabwa, basi mgonero usanachitike, ngati alipo wina amene anabwera kuti adzapemphereredwe, amene angafune kuti apemphereredwe, chabwino, ife tingakhale okondwa kuchita izo pa nthawi ino yokha, ngati alipo aliyense woti apemphereredwe.

883 Chabwino, m'bale, inu mubweretseni iye pamwambapa, izo zikhala bwino. Ndipo mphindi yokha, ndipo kenako ife ti—ife tibalalika. Ndipo kenako ife tikabalalika, ndiye iwo amene akufuna kuti akhalebe pa mgonero, akhoza kutsalira. Koma

pakali pano tipereka pemphero kwa odwala. Kodi Baibulo linanena chiyani?

⁸⁸⁴ Ngati m'baleyo sangathe kudzuka... Izo ziri bwino, ingomusiyani iye akhale pamenepo, ife tibwera kwa iye. Izo ziri bwino, ingomusiyani iye akhale pomwepo. Ndipo titsikira kumeneko ndi kudzamupempherera iye. Izo ziri bwino. Chabwino, bwana, ingo—ingomusiyani iye akhale pomwepo. Ndi zovuta kuti iye ayime apa, bwanji, ife tikhala okondwa kubwera kwa iye.

⁸⁸⁵ Tsopano ine ndikufuna kuti ndipange kulengeza kumodzi kwakung'ono uku, mzanga wokonedwa. Mwaona, ine—ine ndikudziwa kuti Ambuye atsimikizira izi mobwereza ndi mobwereza nthawi zambiri. Mukuona? Ine sindine mlaliki kwambiri, ine ndiribe maphunziro ndi zina zotero. Ine ndimawakonda Ambuye Yesu, Mulungu akudziwa kuti ine ndimamukonda Iye. Koma chinthu chimodzi chimene ine ndinayitanidwira kuti ndizichita, kupempherera odwala. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ngakhale ine ndisanadziwe konse za mphatsoyo, ine ndinkakonda kupita kunja kuno ku chipatala; ndipo ndikukumbukira anamwino amenewo akunena, “Tsopano inu mukhala bwino.” Mukuona? Ndipo basi chinachake, kuti Mulungu wakhala qli wachisomo kulemekeza mapemphero anga kwa anthu.

⁸⁸⁶ Ine ndikulingalira, usikuuno, ngati angaitanidwe, basi kubangala kwa pa dziko lonse lapansi konsekonse mdziko. Ndi kuti, aliyense amene M'bale Branham anamupemphererapo, bwerani kuno, ine ndikufuna kuti inu mupereke yankho ku boma la United States, ndi kalata. Ndipo kumeneko kungakhale kuwulutsa kwa padziko lonse lapansi. Ine ndikuganiza, mwinamwake anthu foro kapena faivi mamillionsi angayankhire kuyitana kumeneko ngati kungadziwike. Mukuona?

⁸⁸⁷ Ndipo anthu amenewo, kapena ena a iwo anali atafa kale, atagonekedwa ndi adokotala, ndipo—ndi woyika maliro. Ena a iwo anaphedwapo mu ngozi; ena a iwo anafa imfa yachibadwa. Ena a iwo ndi akhungu, opinimbira, olumala, opotoka, osautsika, mwaubongo... mzipatala, sanadziwe nkomwe kuti ife tinali m'chipatala kuti tiwapempherera iwo. Kuwabweretsa iwo mkati, amachita kuwatengera mkati. Iwo amakhoza kumenyera njira yawo ndi kudzicheka okha mzdutswa, osadziwa nkomwe kumene iye ali. Mu maminiti faivi, kukhala anthu abwinobwino, okoma, okonda, ndi oganiza bwinobwino masiku awo onse. Mukuona?

⁸⁸⁸ Ndizo... Icho ndi chiyani? Si M'bale Branham. Ndi Yesu Khristu, Iye anandituma ine kuti ndidzapempherere odwala. Tsopano apa ndi chimene icho chiri. Izo sizinakhale zopambana kwambiri mu Jeffersonville, chifukwa, chake ndi chimenechi. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti ine ndiri nawo

ena a abwenzi anga apafupi kwambiri ndi apamtima ali pomwe pano mu mzinda uno. Ngakhale mzindawo pawokha, khalidwe la mzindawo, ine sindimalikonda. Ine sindimakonda zochitika izi, ndipo sindinachitepo; pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, nditakhala, ndikuwerenga mabukhu anga a mbiriyakale, Ine ndinati, "Tsiku lina ndidzachokako kuno." Mukuona?

⁸⁸⁹ Ine sindimakonda Jeffersonville, ndi chithaphwi, chiri pansi kuno. Ndi chithaphwi kwenikweni, ndipo—ndipo ndi zoyipa kwambiri. Mupite kumtunda kuno pamwamba pa Spickert Knobs kapena kwinakwake, ndipo mukayang'ane pansi chaku New Albany ndi Jeffersonville, ngati inu mukufuna kuti muwone. Tawonani apa, madokotala akunena tsopano, kuti, "Anthu a m'chigwa ichi ayamba kuchepa magazi chifukwa cha chochitikacho."

⁸⁹⁰ Dona wamng'ono kuno, Akazi a Morgan, anachiritsidwa ku khansa, anamutengera galu wawo kuno ku chipatala, ankaganiza kuti anali ndi vuto lothothoka ubweya. Inu mukudziwa chimene izo zinali? Kudikha kwa ma Colgate ndi zinthu pa udzu kumene iye anadutsirako. Ndi malo opanda ukhondo kwambiri.

⁸⁹¹ Mnyamata anali mu gulu la ankhondo, anapita kumusi kuno ndipo anakatenga. . . Iye anali ndi mphumu. Anapita kumusi kuno ku Florida ndipo maso ake anada kwenikweni, ndipo iye anapita kwa dokotala, ndipo iye anati, "Dokotala. . ."

⁸⁹² Dokotala anati, "Tsopano, iwe wakhala uli mu ndewu, sichoncho iwe?"

⁸⁹³ Iye anati, "Ayi, bwana, ine sindinatero."

⁸⁹⁴ Ngati inu mukufuna kudziwa kuti ndi ndani, dzina lake ndi Herby. Tsopano, ngati nditangokhoza kungoganiza. . . Ndi—ndi mu Union National Bank, mu New Albany, iye ndi wothandiza anthu. Mudzangopita kumeneko ndipo mukawone amene akuti "Herby," mukamufunse iye.

⁸⁹⁵ Ndipo iye anati. . . Iye anapita, iye anati, "Dokotala," iye anati, "Ine ndiri ndi chimfine."

⁸⁹⁶ Ndipo anamupima iye, anati, "Uko nkulondola." Iye anati, "ine ndimaganiza kuti unali mu ndewu." Anati, "Mnyamata, iwe umakhala kuti?"

⁸⁹⁷ Iye anati, "Inu mwina simungawadziwe malo akewo," anati, "Ine ndimakhala mu mzinda wawung'ono kutsidya kwa Louisville, Kentucky, wotchedwa New Albany, Indiana."

⁸⁹⁸ Anati, "Ukutanthauza kundiuza ine kuti wachitenga chimfine kuchichotsa mmadzi amchere awa kuno ku Miami, kuti chisamabwere?" Anati, "Ngati ungamakhale mu Jeffersonville, Indiana, kapena New Albany, Indiana, iwe ukhoza kukhala

kulikonse padziko lapansi kumene gulu lankhondo la United States lingakutumize iwe.” Ndizo zonse. Mukuona?

⁸⁹⁹ Ndiwo malo opanda ukhondo kwambiri amene alipo mdziko, amene ine ndikuwadziwa, pokhapokha iwo atakhala mu zithaphwi zina za malungo. Mukuona? Ndipo ine—ine—ine—ine ndiri ndi azimzanga pano.

⁹⁰⁰ Tayang’anani kuno, ine ndikhoza kungopita kumakawatchula iwo monga chonchi. Tamuwonani Dr. Sam Adair, mzanga. Chabwino, pali Mike Egan, wakhala pamenepo. Oh, mai, ndi angati amene ine ndingathe kuwatchula! Basi mahandirede a abwenzi abwino kwenikweni, abwenzi anga akale, omwe ine ndacheza nawo. . . Ziribe kanthu ndi abwenzi angati atsopano amene ndawapeza, palibe chimene chingatenge malo a bwenzi lakale. Inu mukudziwa zimenezo.

⁹⁰¹ Apo pali amayi anga okalamba akhala kumbuyo uko, alibe masiku ochulukana pa dziko lapansi, iwo ali mu ma sikisite awo tsopano. Apo pali amayi awo a mkazi anga, sevente, akupitirira ku sevente-wani; akhala kumbuyo kuno penapake, ine ndikuganiza, usikuuno. Ndipo apo, asiyeni iwo. Abambo anga anayikidwa kumtunda kuno; mkazi wanga anayikidwa kunja kuno pa Walnut Ridge; mwana wanga ali kunja uko. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁹⁰² Ine—ine—ine sindimakonda. . . Ine—ine—ine—ine sindikufuna kukhala kuno, ndipo ndikukhulupirira kuti posachedwapa, nthawi yomweyo, ndikuyenera kuchokapo. Mwaona, chifukwa izo zakhala zikubwera kwa ine, ine ndimanena izi pa guwa ndi Baibulo langa, mowirikiza.

⁹⁰³ Pamene ndinamuza mkazi wanga, pamene iwo anatipatsa ife ndalama zomangira nyumba ya abusa ija imene ndinayipereka ku mpingo uno. . . Mpingo uwu ndi mwini wa nyumba imeneyo; mupite kumusi kuno, mukafufuze ngati izo siziri. Mwaona, ine sindikanayitenga iyo inemwini.

⁹⁰⁴ Tsopano, pamene ine ndimati ndikamange kumeneko, Meda anati, “Ine ndikufuna ndizikhala kuno chifukwa cha amayi anga.”

⁹⁰⁵ Ine ndinati, “Wokonedwa, motsimikiza basi monga momwe ife tikufunira, ife tidzakhala achisoni ndi zimenezo. Mwaona, izo sizingagwire ntchito basi. Mulungu anati, ‘Udzilekanitse,’ ine ndikuyenera kuti ndichite zimenezo.”

⁹⁰⁶ Ndipo anati, “Chabwino, amayi anga!”

⁹⁰⁷ Ine ndinati, “Amayi anga, nawonso. ‘Koma iye amene sadzasiya ake omwe, ndipo nkunditsatira Ine, si woyenera kutchidwa Wanga.’ Ndipo izo nzoona.”

⁹⁰⁸ Tsikulina, posachedwapa, ndikumverera kuti ndikuyenera kuti ndidzasunthe, ndiko, kuchokapo. Koma apa pali njira yake, misonkhano singagwire ntchito kuno. Iyo singagwire

ntchito monga imachitira kwina kulikonseko, ndipo aliyense amene anakhalapo pa msonkhano akudziwa kuti izo ndi zoono, chifukwa izo ziri komwe kuno mu mzinda wanga womwe. Ndi zimenezo.

909 Yesu ananena chinthu chomwecho pamene Iye anabwera.

910 Iwo anati, “Kodi munthu uyu ndi ndani? Kodi ameneyo si mnyamata wa kalipentala uja kunja kuno? Kodi anapita ku sukulu yake iti? Kodi anakapeza kuti maphunziro awa? Tsopano ndirole ine ndikuwone iwe ukuchita. . .Iwe ukuti umachita zozizwitsa kuno, ndirole ine ndikuwone iwe ukuchita chinthu chomwecho kuno. Zimene iwe unachita ku Kaperna, ndirole ine ndikuwone iwe ukuchita izo kuno.”

911 Yesu anati. . . “Iye anazizwa ndi kusakhulupirira kwawo.” Iye anapotoloka ndipo anati, “Indetu, indetu, Ine ndinena kwa ina, mneneri samakhala ndi mphotho akakhala pakati pa anthu a kwawo.” Nkulondola uko?

912 Ndipo ife tikudziwa. . . tayang’anani pa. . . Mutengeni Finney, mutengeni Sankey, Moody; mutengeni John Wesley, sakanakhoza nkomwe kupita nazo patali izo, mwaona, mpaka iye atachoka ku dziko lake. Tamuwonani—tamuwonani— a—Moody. Pamene Moody, wosoka nsapato waku Boston, samatha kupita nkomwe, iye anabwera ku Chicago iye asanakhale wotchuka. Mukuona? Iye ankayenera kuzitengera izo kuzichotsa kwa ake omwe. Inu nthawizonse mudzayenera kuchita zimenezo.

913 Koma tsopano, apa, Mulungu adzayankha pemphero ngati mudzaiwale kuti ndi William Branham (Mukuona?), ngati mudzaiwale kuti ndi William Branham ali ndi chirichonse choti achite mu izo, mmodzi yekhayo woti angoyima ndi kukupemphererani inu. Ndi Yesu Khristu amene anachita kale zimene inu mwapempha kuti achite, ngati muti mungokhulupirira izo. Mukuona? Palibe chirichonse choti achite. . . Ine ndiribe kanthu kochita nazo izo, ndikungochitira umboni. Koma zikuwoneka ngati chifukwa ndakulira kuno ndi inu, ndipo mumadziwa kufooka kulikonse komwe ndiri nako, ndi cholakwitsa chirichonse chimene ine ndiri nacho. . . Ndipo inu mukudziwa chimene Mulungu wachita, mu mzinda momwe muno.

914 Mzinda uno, pa Tsiku Lachiweruzo, udzayankha mtengo waukulu tsiku lina, pakuti pakhala pali mahandirede ndi mahandirede a machiritso opambana pomwe pano (Uko nkulondola.), pomwe pano. Zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi kuwonekera kwa Mngelo kumusi uko, ndipo mapepala anzifalitsa ndi chirichonse, ndipo komabe anthu saku. . . Chifukwa chiyani ziri chomwecho?

915 Tsopano tsiku lina, ndidzachokako kuno. Ine ndikudabwa: “Kodi mapeto anga adzakhala otani? Kodi izo zatha? Kodi izo

zangotsala pang'ono? Ine ndiri ndi usinkhu wa zaka forte-eyiti. Kodi zangotsala pang'ono kutha?" Ndikudabwa izi. Ngati izo ziri . . .

⁹¹⁶ Taonani, nchifukwa chiyani dziko silinazindikire chithunzicho pamenepo? Nchifukwa chiyani iwo sanagwire izi mwachangu? Nchifukwa chiyani iwo amalephera kuzigwira zinthu zinazi? Nchifukwa chiyani iwo sakugwira mauneneri awa ndi zinthu? Inu mukudziwa, iwo sangachite zimenezo tsopano, koma tsiku lina ine ndidzachoka padziko lapansi, ndipo pamene ndidzachoka, ndiye iwo adzazindikira Izo. Ena a inu achichepere mudzazindikira izo ine nditapita. Mukuona? Koma Mulungu salola kuti izo zichitidwe pano. Mukuona chimene . . . inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

⁹¹⁷ . . . Ndi chibangiri chabe cha mtsikana wamng'ono. Aliyense akhoza kuchitenga icho. Ndipo ine ndikukhulupirira M'bale Sothmann ananena kuti iye anasiya Baibulo kuno nthawi yotsiriza imene iye anali kuno, ine ndikukhulupirira. Alipo amene anapeza Baibulo, a—Baibulo losochera kuno? Ngati inu munatero, ilo ndi la M'bale Fred Sothmann wochokera ku Canada. Tsopano tiyeni tipemphere.

⁹¹⁸ Ambuye, tichitireni chifundo, pamene nyimboyo iti iziyimbidwa mokoma ndipo M'bale Neville azidzoza mafuta, ine ndipita kukayika manja pa odwala mu Dzina la Yesu. Perekani izi, Ambuye, kwa machiritso awo. Amen.

⁹¹⁹ Aliyense apemphere, tsopano, aliyense. Chabwino.

Ambuye, wamng'onoyo, pamene agogo ake aamuna ayimirira apa chifukwa cha iye. Iye sagwirizana ndi mkaka, mkaka uliwonse. Koma Inu muli nazo Mphamvu zonse ndipo mnyamata wamng'onoyo sangakhale ndi chikhulupiriro mwa iyeyekha. Ndiyeno, Ambuye, ine ndiri ndi chikhulupiriro kwa iye, ndi makolo ndi agogo ndipo ife tikunena, mu Dzina la Yesu, kuti mwana ameneyo akakhoza kumwa mkaka ndi kukhala moyo kwa ulemelero wa Mulungu. Amen. Izo zikhala mwanjira imeneyo.

Oh, Mulungu, iye akuwapempherera abambo ake. Ine ndikupemphera naye iye kuti Inu muwachiritse abambo ake ndi kupereka kwa iwo chimene iwo akuchisowa, mu Dzina la Khristu. Amen.

⁹²⁰ Tsopano, zophweka sichoncho izo? Anthu akupemphera, koma izo ndi zimene anthu . . . Iwo amafunafuna chinthu chachikulu ndipo iwo amazipanga izo kukhala zovuta. Mulungu amaziphweketsa izo. Inu mumazipanga izo kukhala zovuta ndipo mumaziphonya izo. Mukuona? Muzingozipanga . . . Mulole izo zikhale zophweka monga momwe Mulungu ananenera: "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; ngati

iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira,” monga Mulungu ananenera.

⁹²¹ Ife tikuyika manja pa mkazi uyu, Ambuye, mlongo wathu uyu wayima apa, ndipo mulole iye achiritsidwe pamene ife tikupempha izi, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

⁹²² Atate, pamene tikuyika manja pa mlongo wathu, mu Dzina la Yesu Khristu, mu chikumbutso cha Baibulo ndi chiphunzitso cha Ambuye, mulole iye achiritsidwe.

Atate, mu Dzina la Khristu, ife tikupempha machiritso a mlongo wathu, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumupange iye wamphumphu pamene ife tikumvera Mawu Anu, palibe kukayikira kumodzi mmalingaliro anga koma chimene iye angakhale...?...Amen.

⁹²³ Atate, ife tikuyika manja pa mlongo wathu, ndipo tikupempha izo, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti Inu mumuchize iye ndi kumupanga iye wamphumphu. Amen.

Mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikuyika manja pa m'bale wathu ndipo tikupempha kuti Inu mumupange iye wamphumphu kwa ulemelero wa Mulungu.

Atate, mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikumudzoza mlongo, ndipo tikuyika manja pa iye ndi kupempha machiritso ake mu Dzina la Yesu.

Atate Mulungu, ife tikuyika manja pa m'bale wathu, ife tikupempha izo, mu Dzina la Yesu Khristu, pamene ife tikumudzoza iye kuti Inu mumupange iye wamphumphu.

Atate, pano, mkazi wake wokonedwa...?...tikumudzoza iye ndi kuyika manja pa iye, kupempha izo, mu Dzina la Yesu Khristu.

⁹²⁴ Ambuye Mulungu, ife tikumudzoza Edith wamng'onoyu, kuyika manja pa iye, ndipo tikupempha mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu kuti Inu mupereke chopempha chake.

Atate, kwa amayi ake, ifenso tikudzoza ndi kuyika manja pa iye ndi kupempha machiritso ake, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, mulole iye akhale wamphumphu.

⁹²⁵ Atate, ife tikudzoza ngale yamtengo wapatali iyi ya banja ili, kugunda kwa mtima kwakung'ono, mu Dzina la Ambuye Yesu, tsiku lina tinamupereka kwa Iye, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumuchize iye...?...

⁹²⁶ O Mulungu, Inu mukudziwa chopempha cha mlongo wathu ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha chikhulupiriro chake chochilimika. Tsopano, mulole zinthu izo zimene iye wazipempha, kuti...?...iye ankasewera nawo pamene iye ali wamng'ono, ndipo Mulungu, mulole mdani amumasule mkaziyo ndipo mulole iye abwerere kwawo ali bwino, Ambuye. Ife tikumupempherera mwamuna ameneyo, nayenso, amene iye

wamupempha, Inu munalonjeza, “Ngati inu mudzapempha chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke chopempha ichi, mu Dzina la Yesu. Amen. Mulungu akudalitseni inu.

⁹²⁷ Ambuye, pamene mtsempha uwu ukufa pamphumi pa m’bale wanga, tikupempha kuti moyo uphukire, pamene ife tikuyika manja pa iye ndi kupempha izi, mu Dzina la Yesu, kuti mtsempha umenewo ukhale bwino.

Atate Mulungu, ife tikuyika manja pa mlongo wathu titamudzoza iye ndi mafuta, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ife tikupempha machiritso ake. Amen.

⁹²⁸ Atate Akumwamba, monga mlongo wathu waimirira pa zopambana zambiri zimene Inu munazibweretsa, iye akuyimira mmodzi wa wantchito Wanu, mtumiki, wamanjenje kwambiri; mtima wathu wachifundo ukupita kwa iye ife tikudziwa chimene iye amadutsamo. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mumudzoze mlongo wathu chifukwa choyima pano mmalo mwa iye ndi kumudzoza iye chifukwa cha machiritso ake. Ine ndikupemphera, mu Dzina la Khristu. Amen. . . ? . . . Ambuye akudziwa . . . ? . . .

⁹²⁹ Zabwino. Ndine wokondwa kwambiri. Uko ndi kudzoza kwenikweni kwa Ambuye. Ambuye Mulungu, mkazi uyu atapulumutsidwa ku chiwanda chimene wamenyana nacho kwa zaka zambiri, tsiku lina Inu munalola kuti abwere pafupi ndi nyumba uko ndipo kenako Mzimu unatsika, “PAKUTI ATERO AMBUYE,” iye atatha kulira, iye anadzagona pa guwa, iye anali atachita chirichonse chimene iye ankadziwa kuchita kwake, koma izo zinatengera PAKUTI ATERO AMBUYE. Tsopano, iye wabwerera mwana wa mchemwali wake amene akusanza; sakutha kuyenda, wapitirira kale usinkhu wa chaka. Ine ndikupemphera, Ambuye, kuti Inu mupereke madalitso a Mulungu kwa iye mu Dzina la Yesu Khristu. Wokondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo, mlongo, mukuwoneka mosiyana, nanunso. Ndipo muli kutali kwambiri ndi kufa tsopano, sichoncho inu?

Atate Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse mlongo wathu pamene ife tikumudzoza iye ndi kuyika manja pa iye ndi kupempha kuti chinthu ichi chimene Inu munati: “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Iwo adzayika manja pa odwala, iwo adzachira.” Ife tikuvomereza kuti ndife okhulupirira, Ambuye, chotero ife tikupemphera kuti Inu muchite chinachake, mu Dzina la Yesu. . . ? . . .

⁹³⁰ Atate Mulungu, podziwa mtima wa mkazi wamng’ono uyu, monga iye wautsanulira iwo panja, ife tikupemphera kuti Inu mumuchitire iye chifundo ndi kupereka chopempha chimene iye wapempha. O Atate Mulungu, kwa banja lake, kwa ana ake, mnyamata wake, makamaka, Mulungu, ine ndikupemphera


tsopano, kuti Inu mupereke zinthu izi. . . ?. . . ndi mtima wanga wonse, ine ndikupempha izi, mu Dzina la Yesu. Amen.

Atate Mulungu, pamene ife tikumudzoza mkazi yu ndi mafuta, ndi kumupempherera iye mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti Inu mumuchiritse iye ndi kumupanga iye kukhala bwino kwa ulemelero wa Mulungu.

⁹³¹ Dzina lanu silingakhale West, sichoncho ilo?

Atate, ife tikumupempherera dona wamng'onoyu. Iye akuwapemphera adadi ake. Tsopano, ine ndikupemphera kuti Inu muwapatse adadi ake, ali ndi kuitana pa mtima wawo, Ambuye. Iye akufuna kuti iwo apulumutsidwe. Iye sakufuna kuti iwo akhale mu dziko monga iwo ali, yu, mwana wawo yemwe, mphukira yawo. Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mukhale wachifundo kwa iwo, mu Dzina la Khristu.

⁹³² Akudalitse iwe, mwana wanga wamkazi, Mulungu apereke kwa iwe chinthu chimene wachipemphacho.

Wokonedwa Mulungu, ife tikupempherera chifundo kwa iye, ndipo tikupempha kuti Inu mukhale wachifundo, pamene ife tikumudzoza iye. . . . ? . . . 

57-1006 Mafunso Ndi Mayankho Ahebri Gawo III
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org